

KODI MPINGO UDZAPITA CHISANACHITIKE CHISAUTSO?



Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi yokha tsopano kwa mau a pemphero.

² Mulungu Woyera kwambiri ndi wolungama, ife tikufuna kuti tikuthokozeni Inu chifukwa cha chifundo Chanu chokonda, pakuti icho ndi chabwino kwa ife kuposa moyo. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mukomane ndi ife usikuuno mwa njira yapadera kwambiri, ndi kutipatsa ife za madalitso Anu. Mulole ife tiwone dzanja lalikulu lotambasulidwa la Mpulumutsi wathu wokonda, kuti litumikire kwa odwala ndi kwa osautsika. Ndi kupereka dzanja lolandira kwa iwo omwe ali otopa mu msewu wa tchimo, usikuuno. Kutu muwaitanire iwo ku nyumba ya Atate kumene iwo akuyembekezedwa kuti akakhaleko.

³ Ife tati tikupempheni Inu kuti muwakumbukire iwo omwe achoka ku khwalala ndi njira yopapatiza, kuti iwowonso akhoze kubwerera ku chiyanjano cha Atate kachiwiri.

⁴ Ndipo ife tikupemphera, usikuuno, Ambuye, kuti Inu mutsegule makutu a anthu, kuti awumve Uthenga, ndi kuti Inu mudule milomo ya woyankhula. Ndipo mutilole ife tingogwiritsidwa ntchito kwa ulemmerero Wanu. Ndipo pa mapeto a msonkhano uno, pamene ife tizipita ku malo athu osiyana, mulole ife tizinena monga iwo omwe anabwera kuchokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula ndi ife munjira muja?” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Mwana Wanu, Ambuye Yesu. Amen.

⁵ Ine ndikukhumba kuti ndiwerenge zina zochokera mu Malemba usikuuno, mutu wa 17 wa Luka Woyera, ndi kuyambira ndi—ndime ya 26.

Ndipo monga zinaliri mu masiku a Nowa, chomwecho zidzakhalanso ziri mu masiku a Mwana wa munthu.

Iwo anadya, iwo anamwa, iwo anakwatira akazi, iwo anaperekedwa mu ukwati, mpaka tsiku lomwe Nowa analowa mu chombo, ndipo chigumula chinadza, ndipo chinawawononga iwo onse.

Mwa mchitidwe womwewonso monga izo zinali mu masiku a Loti; iwo anadya, iwo anamwa, iwo anagula, iwo anagulitsa, iwo anabzala, iwo anamanga;

Koma tsiku lomwelo limene Loti anatuluka mu Sodomu...moto ndi sulfure zinavumba kuchokera kumwamba, ndipo zinawawononga iwo onse.

Ngakhalenso chotero izo zidzakhala ziri mu tsiku pamene Mwana wa munthu ali kuululidwa.

⁶ Ndipo kwa nkhaniyo, ine ndikukhumba kuti nditenge kuchokera pa Genesis, mutu wa 19 ndi—ndime ya 22.

Fulumira *uwe*, ndipo bwera kuno; *pakuti ine sindingakhoze kuchita* kanthu *mpaka uwe utabwera kuno.*

⁷ Mmawa uwu, ine ndinali kuyankhula za ziweruzo zomwe ziri kudza, ndipo usikuuno ine ndikukhumba kuti ndipitirize. Ife tikukhoza kumverera mphepo zotentha za chiweruzo choyandikira cha Mulungu Wamphamvuzonse. Pamene ife tikuyamba kumverera zinthu izi, izo zikutikakamiza ife kukhala ngati tiziyang’ana pamene ife tiri kukhala moyo, ndi ora lomwe ife tiri kudutsamo.

⁸ Ndipo nthawiyina kale, unali mwayi wanga kuti ndikacheze ku India. Ndipo basi ine ndisanafike ku India, iwo anali ndi chivomezi chachikulu. Ndipo ine ndinali kuwerenga mu nyuzipepala ku India, za momwe kuti pafupi masiku awiri chivomezi chisanabwere, izo zinkawoneka kuti ankadziwa kuti chinachake chinali chitalakwika; mbalame zazing’ono zonse zomwe zimakhala mu ming’alu ya zinyumba zazikulu, ndi zokhala mu makoma aakulu amiyala monse. Kochuluka kwa India ali nao makoma a miyala. Ndipo mbalame zazing’ono zonse zomwe zinali ndi zisa zao mu ming’alu imeneyo, zinachoka ku makomawo. Ndipo ng’ombe zonse zomwe kawirikawiri zinkaima mozungulira nyumba zazikulu, madzulo, mu mthunzi, ndi kuzungulira makoma aakulu amiyala, kwa pafupi masiku awiri chisanachitike chivomezi, zinyama zonse izi ndi mbalame zazing’ono zinapita pakati pa munda kukaima.

⁹ Inu mukuona, panali chinachake cha izo, kuti Mulungu anali akusamalira mbalame Zake zazing’ono ndi zinyama Zake. Inu mukudziwa, Mulungu yemweyo yemwe anazilondolera izo kukalowa mu chombo, mu masiku oyambirira, pamene iwo anawonongedwa ndi madzi, mwa kulalikira kwa Nowa, Mulungu yemweyo akanali moyo ndipo akulamulira lero, ndipo Iye ali nao ulamuliro Wake pa zokhalapo Zake.

¹⁰ Ndipo ine ndinali kuganiza, “Ngati Mulungu anali wolingalira kwambiri za mbalame Zake zazing’ono, ndi ng’ombe Zake ndi nkhosa, kuti azichotse izo ku chiwonongeko icho chisanakanthe, ali wolingalira mochuluka bwanji za ana Ake omwe abalidwa ndi Mzimu Wake, otsukidwa mu Magazi Ake. Iye ali wolingalira kwambiri za iwo.” Ndipo monga Iye anazichenjeza mbalame zazing’ono kuti zichoke ku malo awo okhalamo, ine moonadi ndikukhulupirira kuti Iye akuwachenjeza anthu Ake, lero. Pamene ife tikuwona zizindikiro zazikulu za Kudza Kwake ziri pafupi, ine ndikukhulupirira kuti Mulungu akuwachenjeza anthu Ake kuti

abwere palimodzi, ndi kuitana kwakukulu kuti atuluke mu tsiku lotsiriza lino.

¹¹ Phunziro langa usikuuno ndilo: *Kodi Mpingo Udzapita Chisanachitike Chisautso?*

¹² Tsopano ndi mochedwa kuposa momwe inu mukuganizira. Ndi mochedwa kwambiri, mpaka ine ndikukhulupirira kuti ziri pafupi mochedwa kwambiri mu Amereka. Ife tiri basi pa mapeto a msewu. Ndipo mmawa uno, pamene ine ndinali kulalikira za Babeloni ndi zikhaliidwe zake, ine ndinaganiza kuti chikanakhala chabwino kwambiri usikuuno, kuti ndibweretsemo zina za mu Baibulo, kuti ndikusonyezeni momwe ife tiriri oyandikira ku Kudza kwa Ambuye. Ndipo ife tikhoza kuwona, ife ndi diso lathu lachibadwa, kuti chinachake chiri kukonzekera kuti chichitike.

¹³ Pali zoterozo—zisokonezo pakati pa anthu, ndi zovuta basi kuti uyesere kukhala ndi chitsitsimutso. Mpingo ili yosiyana kwambiri, ndipo ili pa makosi a wina ndi mzake, chifukwa cha malire a za chipembedzo. Ndipo Akhristu ali amanjenje kwambiri, zikuwoneka ngati, ndi okwiya. Koma, inu mukudziwa, ndi zachilendo, koma Ambuye wathu anati, “Pamene zinthu izi ziziyamba kuchitika, kuti tiziyang’ana mmwamba,” nati chiwombolo chathu chiri kuyandikira.

¹⁴ Ndipo pamene ife tikuwona chifundo Chake chachikulu, pamene icho chikufikitsidwira kwa ife, kuwona manja Ake a zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa; zomwe, maso athu ati atsegulidwe, mu maminiti pang’ono, kuti tipenye. Ndiyeno izo zikutipatsa ife chithonhozo cha kachetechete ichi, podziwa kuti Mulungu wa Baibulo akadali ndi moyo lero. Ndipo Iye amawakonda ana Ake, ndipo Iye akuwapatsa iwo chenjezo. Ndipo iwo omwe ali a malingaliro—auzimu, akutulukamo.

¹⁵ Ndipo ife tikuzindikira, mu tsiku lomwe Yesu anali kulikamba, Iye anati, “Monga izo zinaliri mu masiku a Nowa, ndi mu masiku a Loti.”

¹⁶ Tsopano, pa mphambano iliyonse ya nthawi, Mulungu wakhala nthawizone akupereka kuitana kwa chifundo kusanachitike kuitana kwa chiweruzo.

¹⁷ Tsopano ngati muli azambiriyakale, ndipo ine ndakhala ndikuwerenga mbiriyakale sabata ino, ndi masabata awiri kapena atatu apitawa, Ante-Nicene Fathers, la mbiriyakale yamakedzana ya mpingo basi isanachitike Khonsolo ya Nicene, ndiyeno anali akuupanga mpingo wa Katolika mu zaka fiftini handiredi za mibadwo ya mdima. Ndipo ine ndikuwona kuti mu zolemba za Nicene izo, kapena Khonsolo ya Nicene Isanachitike, kuti iwo anali nazo chimodzimodzi basi monga ife tiri lero. O, momwe izo zimadzibwerezera zokha!

¹⁸ Ndipo kuti uwone chikhaliidwe cha mpingo, ndi chikhaliidwe cha anthu, ndi zizindikiro za nthawi, izo zalembedwa paliponse.

¹⁹ Tsopano, Mulungu asanati achite chirichonse, pa mphambano iliyonse ya nthawi, Iye nthawizonse amatumiza chifundo, mngelo, mneneri, Uthenga. Ndipo monga nthawi iliyonse, komabe, zonse izo zakhala zikukanidwa. Mpingo sumafuna kuti uzilandira Izo.

²⁰ Nowa. Iye anayankhula za Nowa apa. Ndipo iye analalikira zaka handiredi ndi twente. Ndipo ngakhale uthenga wake unali chifundo, anthu analephera kuti amvetsere chiphunzitso chake. Icho chinali chinachake chimene chinali choti chiwapulumutse iwo, ndipo komabe iwo sanati amvetsere ayi. Ndipo ngati icho sichiri chithunzi chokongola kwambiri cha nthawi ya lero!

²¹ Tsopano, inu mukhoza kunena kwa ine, “M’bale Branham, inu mungakhoze bwanji kuti ‘zokongola,’ ndi kumajambula chithunzi kwa ife chomwe inu mukujambulachi?”

²² Ndi zokongola chifukwa Ambuye Yesu akubwera posachedwapa kwa Mpingo Wake, ndipo ndilo lingaliro lokongola kwambiri lomwe cholengedwa chirichonse cha Mulungu chingakhoze kuchilingalira; kuti tichoke mu chisokonezo ichi ndi kukalowa mu Ulemerero Wake wodala, komwe aakulu ati adzakhale aang’ono, ndipo odwala adzakhala ochiritsidwa kwanthawizonse. Kudzakhala kuli kopanda zisoni zina kapena kupweteka mtima. Ngati icho sichiri chinthu chokongola kwambiri chomwe ine ndingakhoze kuchilingalira! Ndi kudalitsa kwake momwe ziriri kwa iwo omwe akudikirira nthawi yakusonkhana iyo.

²³ Tsopano ife tikupeza kuti, monga Yesu analozera mmbuyo ku masiku a Nowa. Tiyeni tingobwerera mmbuyo, chifukwa Iye anati, “Titengere chitsanzo cha tsiku limenelo.”

²⁴ Tsopano, pamene Kaini ndi Abele. Pamene Kaini anamupha Abele, ndiyeno Seti anatenga malo ake. Ife tikupeza kuti Satana anali kuyesera kuti ayiwononge Mbewu iyo yomwe ikanati idzabwere, yomwe Mulungu anali atalonjeza, kuti, “Mbewu ya mkazi ikanati idzavulaze mutu wa mbewu ya serpenti.” Ndipo Satana anali kuyesera kuti aiwononge Mbewu yachifumu imeneyo, ndipo iye ankaganiza kuti anachita izo pamene iye anamuwononga Abele. Koma Mulungu anautsa Seti m’ malo ake. Chithunzi chokongola kwambiri cha kufa ndi kuuka kwa Khristu, ndi kudza kwa Mbewu yachifumu.

²⁵ Ndiye nchoti nkukambapo kuzindikira kuti momwe, ku mbali ya Kaini, iwo anakhala achipembedzo kwambiri. Ndipo iwo anali anthu opita-kutchalitchi; ndipo chomwechonso Kaini anali munthu wopita-kutchalitchi. Iye ankawapembedza Ambuye. Iye anamanga guwa. Iye anali wa pa mpingo. Iye ankalipira ngongole zake. Iye anali, mwa njira iliyonse monga munthu akanakhoza kuyang’ana pa iye, kukhala ali wokhulupirira weniweni.

26 Koma alipo magulu atatu okha a anthu, ndiwo, okhulupirira, osakhulupirira, ndi odzipangitsa-kukhulupirira. Ndipo dziko likadali lodzaza ndi iwo usikuuno.

27 Ndipo Kaini anali kungodzipangitsa kukhulupirira. Ndipo kuchokera mu mndandanda wake munadza gulu lalikulu la anthu opita-ku tchalitchi, achipembedzo kwambiri.

28 Tsopano, izi ndi zosazoloweka kwambiri, koma kodi inu mumazindikira kuti kuchokera ku mbali yake kunadza mtundu wa anthu otukuka, ophunzira? Baibulo limafotokoza izo mwachimvekere. Iye anati, “Iwo anali kumanga, ndipo iwo anali kuchita zinthu zazikulu.” Sayansi inabwera kupyolera mu mndandanda wa Kaini. Ndipo asayansi aakulu, ndi madotolo, ndi anthu aakulu, anabwera kuchokera mu mndandanda wa Kaini.

29 Pamene, mbali inayo inali y—yosauka, anthu a mtundu-waumphawi, koma iwo anali anthu omwe ankamukhulupirira Mulungu wawo kuti anali weniweni. O Mulungu, mundiwerengere ine ndi iwo!

30 Ndipo basi nthawi yotsiriza isanafike, panali chisokonezo chachikulu. Ndipo mbali yaikulu ya mpingo, inkawoneka ngati, inali itapambana, basi monga izo ziriri lero, chifukwa cha sayansi.

31 Ndipo chinthu china chachikulu, iye anati, “Iwo anali kumanga.” Sipanayambe pakhala nthawi mu mbiriyakale yomwe kumanga kwakhala kwakukulu kwambiri monga kuliri tsopano. Ndi chimodzi cha zizindikiro cha nthawi yotsiriza. Sitinayambe takhalapo nayo nthawi yomanga. Ndipo tsopano, ngakhale mu mzinda wathu waung’ono uwu kuno, ine sindikumakhoza kupeza malo okwanira kuti ndizipita kukasaka akalulu panonso. Konse kwangokhala ntchito zomanga; kumangomanga ndi kubzala. Ndipo ngati ife tikanati titsegule maso athu, ndi chimodzi cha chizindikiro cha Mulungu choti mapeto ali pafupi.

32 Ndipo ife tinali kulalikira mmawa uno, za ma sputnik ndi mizinga, momwe iwo angakhoze kuima mu Moscow, ndi kulunjika mzinga pakati pa Fourth Street mu Louisville, ndipo nkusachoka nkomwe mu Moscow. Ndipo iwo unghaphulitse chibowo mu nthaka, mapazi handiredi-ndi-sevente-faifi kuya kwake, la mailosi handiredi ndi fifite kuzungulira ilo. Ndiko kukula kwake bowolo lingati likhale. Itatu ya iyo ingawononge dziko lonse, kuligwedeza ilo kuchoka mu njira yake. Sayansi, inu mukuona mbali yomwe iyo iriko? Iyo iri ku mbali ya oyipawo.

33 Mulungu akuyembekeza kuti ana Ake kuti azimudalira Iye pa chirichonse chomwe iwo ali nacho. Koma ife timafuna kuti tizidalira dzanja la munthu. Ine kuli bwino ndikhale ndi ziyembekezo zanga zitamangidwa mwa Khristu, kutenga kuima kwanga kwaulemu pa chisomo Chake ndi chifundo, kuposa

gulu lophunzira lirilonse la anthu omwe angati apange bungwe, nkumati, “*Iyi* ndiyo njira.” Khristu anati, “Ine ndine Njira, Choonadi, ndi Kuwala. Ndipo palibe munthu amadza kwa Atate kupatula iye atadzera mwa Ine.”

³⁴ Chotero, inu mukhoza kuwona, ndi tsiku lalikulu la maphunziro. Ndi tsiku lalikulu la mkangano wa mdziko. Ndipo mkati momwe mwa izo, iwo ayenera kuti anali ndi dziko la sayansi yaikulu kuposa yomwe ife tiri nayo tsopano. Iwo ankamanga mapiramidi. Ife tiribe chinthu chimodzi chomwe chingamange piramidi, ngati inu munayamba mwayandikirapo izo. Ine ndakhalapo ndiri pa izo, mu Igupto, ndipo izo za mu Mexico. Ndipo zazitali, kutalika ngati midadada ya mu mzinda, zimakhala ziri zimiyala zomwe zingalemere mpaka matani mazana, zitamangidwa pamwamba apo pamwamba pa, chimango chachikulu icho. Ndipo izo zinkadulidwa mwangwiro kwambiri mpaka sipamakhala ngakhale malo a lumo; izo zinkadulidwa mwa ukatswiri. O, tsiku lake la sayansi! Ndipo, aponso, izo zinaikidwa mwangwiri kwambiri pakati pa dziko lapansi, ndipo ziribe kanthu kuti dzuwa liri kuti, sipamakhala konse mthunzi kuzungulira iyo. Ine ndikukaika ngati ife tingafanane ndi izo, lero, mu sayansi yathu yamakono.

³⁵ Koma Yesu anati, “Monga izo zinali mu tsiku ilo, chomwechonso izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa Mulungu.” Tsopano, ndipo Nowa analalikira zaka handiredi ndi twente, ndipo, zindikirani, iye anali kusekedwa.

³⁶ Tsopano, Yesu nayenso anati, kuti, “Monga izo zinali mu masiku a Loti, kuti, izo zikanadzakhala.” Mu masiku a Loti, iwo anali kudya, kumwa, kukwatira, kuperekedwa mu ukwati, kukonzekera, kumanga, kugulitsa, kugula.

³⁷ O, silinayambe lakhalapo tsiku, lomwe, zamalonda zochulukuka kwambiri, monga lero, malo a magalimoto ogwiritsidwa kale ntchito ndi zirizonse. Zochulukuka kwambiri, mpaka, inu mukhoza kugula firiji chaka chino, ndi kulipira pafupi madola foro kapena faifi handiredi pa iyo, ndipo chaka chamawa palibe yemwe angaifune iyo. Iyo yachoka mu sitailo. Kodi inu simukuwona kumene dziko lamalonda layika mphuno yanu ku gudumu loperera? Iwe ukhoza kugula galimoto chaka chino, ndipo chaka chamawa iyo ndi yabwino basi monga yomwe iwe ukanaigula apo, koma iyo ikanakhala itatsika mtengo ndi madola sauzande chifukwa iwo asintha chivindikiro cha pothirira madzi kapena iwo anachita chinachake chopusa chaching’ono kwa iyo. Ndi nkhani yazogulitsa basi, kuti akwaniritse Baibulo.

“Monga zinaliri mu masiku a Nowa, ndi mu masiku a Loti.”

³⁸ Ngakhale, nthawi iliyonse, angelo ankawonekera, aneneri ankaukapo, ndipo uthenga wawo nthawizonse umakhala uli chisomo, chifundo, ndi chiwombolo. Uthenga wa Mulungu

nthawizonse wakhala uli chiwombolo, basi isanafike nthawi yotsiriza. Zifufuzeni izo kupyola mu Malemba. Momwe Nowa analalikirira chiwombolo, ndipo iwo ankawaseka iwo ndi kuwaseleula iwo, ndipo iwo ananyogodoledwa.

³⁹ Ndipo monga izo zinali mu masiku amenewo, chomwechonso izo ziri lero. Ndipo pamene inu mupita nao Uthenga, kuti Khristu wauka kwa akufa, monga Iye analonjezera kuti Iye akanadzadziwonetsa Yekha apo. Ndipo iwo akuchita lero, kwa uthenga umenewo, chimodzimidzi monga iwo anachitira kwa Uthenga mu tsiku linalo.

⁴⁰ Loti anapita mu Sodomu, ndipo anayesera mwakukhoza kwake kuti awatengere abale ake kuti amvetsere ku uthenga wa Mngelo, koma iwo anamutonza iye ndipo ankati iye anali kupanga zosangalatsa.

⁴¹ O, chithunzi chake cha tsiku ili! Pamene iwe ubweretsa kwa iwo Uthenga wa chiwombolo cha Mulungu, iwo amati, “Iwe ukunyojetsa chipembedzo. Iwe ukuyesera kusanzira chinachake.” Mtundu womwewo wa gulu! Ora lake lomwe ife tiri kukhalamo! “Chabwino, iwo akuganiza kuti ndi iwo okha omwe ati apulumutsidwe. Iwo akuganiza kuti ndi iwo okha omwe akulalikira Uthenga.”

⁴² Yesu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Awo si Mawu anga. Iwo ndi Mawu Ake.

⁴³ Ndipo zindikirani, ine ndikufuna inu kuti muzindikire, mwamsanga, mtundu wa uthenga womwe iwo unali. O, izi zimangokondoweza mtima wanga. Pamene ine ndiganiza za Sodomu ndi Gomora, anali ataipitsidwa kwambiri, mwamakhalidwe, mpaka zosokonezeka zinali paliponse.

⁴⁴ Koma basi chiwonongeko chotsiriza chachikulu, chisanafike, Mulungu anatumiza mneneri kumeneko. Ndipo ine ndikuganiza, za kutinso, Iye anatumiza Mngelo kumusi uko, ndipo ine ndikufuna kuti inu muuzindikire Uthenga wa Mngeloyo. Abrahamu, yemwe anali atatenga njira yake ndi okanidwa apang’ono a Ambuye, iye anauyamba waku chipululu kumene nthaka inali yosauka.

⁴⁵ Ndipo Loti anapita uko ndipo anakakhala mfumu ya mzinda, ndipo iye anali munthu wamkulu pakati pa tchimo. Ine kuli bwino ndisakhale wotchuka kwambiri, ndi kukhala mwabwino ndi Mulungu. Koma Loti anali wotchuka kwambiri, ndipo iye anakakhala ku misewu, ku chipata cha mzinda. Iye anali woweruza wa chomwe chikanalowa umo ndi chomwe sichikanati chilowe umo. Ndipo uko iye anali, akupereka moyo wake ku ziwerewere, ndi kumadziwa kuti mu mzinda wake zinthu zoterozo zinali zikuchitika.

⁴⁶ Ngati icho sichiri chithunzi cha lero, mu fuko lathu; maprogramu osapimidwa, mitundu yonse ya zopusa, kuuma mtima, uthakati! O, iwo akanakhoza kuzileketsa izo, ngati

iwo akanafuna kutero, koma iwo sakufuna kutero. Ndipo iwo sangakhoze kuchita izo, chifukwa Mulungu anati iwo zikanadzakhala ziri mwanjira iyi. Ngati iwo akanangokhoza kutsegula maso awo ndipo akanakhoza kumvetsa!

⁴⁷ Ndipo, zindikirani, basi ora lalikulu lovuta lisanafike. Abrahamu ndi Sarah, omwe anakhala uko pansi pa mtengo wa thundu, tsiku lina pamene iwo anali panja apo, Sarah anawaona Amuna ena akubwera. Ndipo iye anauyamba waku hema.

⁴⁸ Kusiyana kwake, kwa akazi a lero, ndi momwe zikanakakhalira zosiyana uko mu Sodomu. Ikafika nthawi yoti amuna akubwera kunyumba, iwo onse amakavala zovala zawo zomasuka zazing'ono, ndi kupita panja nkukatenga chotchetchera pabwalo. Kusiyana kwake!

⁴⁹ Koma Sarah anapita ku hema. Ndipo pamene iye anatero, Amuna awa anabwera uko. Ndipo Abrahamu anayang'ana pa Iwo. Iwo ankawoneka kuti anali maka Amuna owoneka-mwachilendo. Ndipo mmodzi wa iwo ankawoneka kuti anali wowayankhulira, ndipo pamene Iye anakhala pansi ndipo Iye atayamba kuyankhula ndi Abrahamu.

⁵⁰ Abrahamu anati, “Khalani pansi apa, ndipo ine ndipita ndikatenge madzi pang'ono, ndipo ine nditsuka mapazi Anu. Ndipo ine ndiphika mkate waung'ono. Ndipo ife tikhala okonzeka, ndipo Inu mukhoza kudya nthuli ya nyama. Ndiyeno Inu mukhoza kumapitirira.”

⁵¹ Ndipo pamene iye anathamangira kunjira mu gulu la ziweto, ndipo anakapeza ng'ombe yonenepa, ndipo anaipha iyo. Anamuza Sarah kuti akanyange za mkate pang'ono ndi kupanga makeke ena.

⁵² Ndipo iye ankayankhula kwa Mwamunayo. Ine ndikukhulupirira kuti, mwanjira ina kapena imzake, Abrahamu ankadziwa Yemwe uyo anali. Ndipo Munthu yemwe anali woyankhula, anali ndi nsana Wake atautembenezira ku hema. Iye anali Mtumiki wa tsiku limenelo. Ndipo Iye anati, “Abrahamu, ine ndidzakuchezera iwe malingana ndi lonjezo, zaka twente faifi zisanachitike. Ine ndinapangana nawe lonjezo, ndipo ine ndikhala ndiri nalo.”

⁵³ O, lidalitsidwe Dzina la Ambuye! Mulungu anapanga lonjezo, “Mu masiku otsiriza, Iye akanati adzatsanulire Mzimu Wake pa mnofu wonse,” ndipo Iye akhala ali nalo. Yesu anapanga lonjezo, ndipo anati, “Zinthu zomwe Ine ndikuzichita muzidzazichita inunso,” ndipo Iye akhala ali nalo, pakuti Iye ndi wolungama.

⁵⁴ Ndipo Abrahamu anayang'ana pa Iye. Ndipo Iye anati, “Pafupi nthawi ino basi mwezi wa mawa, malingana ndi moyo,” izo zinali kwa Sarah, “Ine ndati ndidzakuchezereni inu, ndipo Sarah ndi woti adzabala mwana yemwe ine ndinamulonjeza.”

Tsopano, Abrahamu anali usinkhu wa zaka handiredi, ndipo Sara anali nainte.

⁵⁵ Ndipo Sarah, kuseri kwa Mngelo, mkati mwa hema, anapita... anaseka.

⁵⁶ Ndipo Mngelo, ali ndi msana Wake utatembenezidwa, anati, “Chifukwa chiani Sarah anaseka?” Ameneyo anali Mtumiki. [M’bale Branham akugogoda pa guwa kasanu ndi kawiri—Mkonzi.] O, kodi inu mukudziwa zomwe ine ndikuzikamba? Kunali kuweringa kwa maganizo kwa mtundu wanji kumeneko, ali ndi nsana Wake atautembenezira ku hema, ndi iye mkati mwake? Ndipo iye anamwetulira. Ndipo Iye anati, “Chifukwa chiani iye waseka?” Iye anazidziwa izo. Ndipo uwo unali Uthenga wotsiriza Sodomu ndi Gomora asanawotchedwe. M’bale, ngati inu mukuumvetsera Iwo, usikuuno, uli tsopano Uthenga wotsiriza dziko ili lisanawotchedwe. Mwachiona chikhalidwe cha Mngelo? Mngelo uja anali ndani? Iye anali Mulungu.

⁵⁷ Kumbukirani, Abrahamu anamutcha Iye, “Ambuye.” Ndipo kumasulira pamenepo ndi “Elohim, wamkulu, Yehova wamphamvu.” Uyo anali Yesu Khristu atavala thupi linanso.

⁵⁸ Wina anati, “Kodi inu mukutanthauza kunena kuti uyo anali? Kodi iye analipeza bwanji thupi limenelo?”

⁵⁹ Bwanji, Iye anangowaitana Angelo awiri aja. Ndipo anapumira mpweya pang’ono, monga *choncho*, ndipo maatomu ndi kalsiamu ndi potashi zinabwera palimodzi, ndipo Gabrielo analowa mu limodzi, ndi Mngelo wina mu linalo. Ndipo Iye anadzipangira limodzi la Iyemwini.

⁶⁰ Lidalitsike Dzina Lake loyera! Ndine wokondwa kwambiri, usikuuno, kudziwa kuti Mulungu yemweyo Wamphamvuzonse, Yemwe akanakhoza kudzipangira Iyeyekha thupi loti azikhalamo, chidaliro changa chiri mwa Iye, kuti tsiku lina Iye adzaliukitsa ili, monga Iye analonjezera kuti adzatero.

⁶¹ Ndipo Iye ali pakati pathu, akuchita chinthu chomwe chomwecho chimene Iye anachichita uko. O, litamandike Dzina Lake laulemerero; kutipatsa ife chenjezo, kuyankhula kwa ife, kuti uza ife kuti tikonzekere. Ndithudi, Iye anati, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko siliti lindiwonenso Ine. Komabe, inu muzidzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka kumapeto a dziko.” Ndi ora bwanji lomwe ife tiri kukhalamo!

⁶² Zindikirani, Mngelo yemwe anabweretsa moto, anali Mmodzi Yemwe anachita chozizwitsa chija. Ndipo ife tonse tikudziwa kuti dziko likuti lidzawonongedwe, nthawi yotsatirayo, ndi moto. Ndipo Mngelo yemwe anatumizidwa ku Sodomu ndi Gomora... Penyani chimene Yesu ananena. O, izo zimangokondoweza moyo wanga ndikafika pa izo. “Monga zinaliri mu masiku a Nowa, chomwecho izo zidzakhala ziri pa

kudza kwa Mwana wa munthu.” [M’bale Branham anagogoda paguwa kaseveni—Mkonzi.] Kodi Mngelo uja anachita chiani? Iye anali ndi mzimu wa kuzindikira za mu mtima. Ndipo Iye anati, “Monga izo zinaliri apo, chomwecho izo zidzakhala ziri pamene Mwana wa munthu adzakhala akuululidwa kuchokera Kumwamba.” Kodi inu mukuziwona izo? Tangoganizani, kuti, pakati pathu tsopano paima Mngelo yemwe uja wa Mulungu, yemwe sali winanso koma Ambuye Yesu Khristu, mu mawonekedwe a Mzimu Woyera. Ali pakati pathu, “Mu tsiku limenelo.” Ndipo Iye anali Mulungu, ndipo umenewo unali Uthenga Wake chiwonongeko chisanafike kumene.

⁶³ Tsopano ife tikuzindikira kuti unali Uthenga wa chiwombolo. Iye anapita uko ndipo anakayesera kuti awawombole anthu, ndipo iwo anakana kuti amvetsere kwa Iye.

⁶⁴ Ndipo, lero, ndi chinthu chomwecho mu fuko lathu, pakati pa anthu athu. Ine ndakhalapo nawo mwayi wa kuwawona Ambuye Yesu, mu misonkhano, akuchita zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zinthu zazikulu. Ndipo anthu anachita kumaimadi pa nsanja ndi kumadziwa, kupyola mthunzi wa chikaiko, kuti—kuti Mulungu wamkulu, wachisavundi, wopandamalire ali pamenepo ndipo akuchita mtundu womwewo wa chozizwitsa; ndipo iwo amaima pamenepo ndi kumatafuna chingamu, ndi kuyenda kuchoka pa nsanjapo, osakhudzidwa. Iwo samasamala.

⁶⁵ Izo zimawoneka kwa ine, monga, ngati munthu akhala nao mtundu uliwonse wauzimu pa iye, kapena Mzimu wa Mulungu mwa iye, ndipo pamene iye awona Ambuye Yesu akuchita basi zomwe Iye analonjeza kuti Iye akanati adzachite, izo zikanati zikondoweze mtima wake mwanjira yotero, mwakuti iye sakanakhoza kusunga mtendere wake motalikiranso. Iye angaliyatse fuko ndi moto wa Uthenga. “Monga izo zinaliri mu masiku amenewo,” Iye anati, “chomwecho izo zikanati zidzakhale.”

⁶⁶ Uthenga uwo unapita konse, ndipo iwo ankangowuseka chabe iwo ndi kunyogodola pa iwo, ngati winawake yemwe anali kunena mtundu wina wa nkhani yopandapake. Koma iwo unali wa chifundo, ndipo iwo unali wa chisomo, ndipo iwo unali wa chiwombolo. O, mai!

⁶⁷ Ndipo Mngelo ananena, mmawa uja, kwa Loti, Iye atatha kupereka uthengawo; Iye anati, “Fulumirani, bwerani kuno, pakuti ine sindingakhoze kuchita kanthu mpaka inu mutabwera kuno.” Ine ndikufuna kuti inu muzindikire ichi tsopano, pakuti ife tiyenera kudula mofupikitsa apa, pa chifukwa cha mzere wa pemphero. Kodi inu munazindikira chimene Mngelo ananenacho? “Ine sindikhoza kuchita kanthu mpaka inu mutabwera kuno.” Chinali chiani icho? Uwo unali uthenga wa chiwombolo. Ndipo chidutswa chimodzi cha moto chisanagwe

kuchokera Kumwamba, Loti ankayenera kuti atulukemo mu Sodomu.

⁶⁸ Ndipo dontho limodzi la mvula lisanagwe kuchokera Kumwamba, Nowa analowa mu chombo.

⁶⁹ Ndipo bomba la atomu lisanakanthe fuko lino, Mpingo udzapita mu Mkwatulo, kuti ukakomane ndi Ambuye Yesu. Ndipo momwe ma sputnik ndi mizinga zayikidwa, ndipo zowombera zakokedwa, Angelo onse aima mu dongosolo. Aleluya! Makonde aakulu a Kumwamba adzazidwa ndi unyinji. Azeze onse akungidwa. Mabandi aakulu aphunzira kale. Pali nthawi Yakubwera kwathu posachedwapa, kwa Mpingo wa Mulungu wamoyo, yemwe wakhala akuyembekezera Kudza Kwake. Chirichonse chiri mu dongosolo. Ndine wokondwa kwambiri. Ine ndikuyamba kutopa kwambiri. O, kufuna ora lalikulu ilo!

⁷⁰ Ndipo kuganiza, kuti, ife takhala nalo gawo mu mphambano iyi ya nthawi! Kumbukirani, “Chomwecho izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu, pamene Mwana wa munthu ali kuululidwa kuchokera Kumwamba.”

Tsopano, kumbukirani, mvula isanagwe, Nowa anali mu chombo.

⁷¹ Moto usanagwe, Loti anali atatuluka mu Sodomu. Chifukwa, Mngelo anati, “Ine sindingachite kanthu mpaka iwe ubwere kuno. Ine ndiri ndi chokhethemulira mu dzanja langa, kuti ndichikoke ndi kupangitsa moto kuti ugwe kuchokera Kumwamba.”

⁷² Ndipo ine ndikuganiza izo ziri ndendende. Mngelo wa chiwonongeko waligwira dzanja la Russia, limodzi ndi mabomba a atomiki; mpaka Mpingo ubwere palimodzi, ndi Thupi limodzi lalikulu la Khristu. “Ine sindingakhoze kuchita kanthu mpaka iwe utabwera kuno.” O, ngati icho sichiri chitsimikizo chodala!

⁷³ Ndipo pamene ife tikuwona chirichonse chitaikidwa mu dongosolo, kupita Kwawo kwa Mpingo kuli mu dongosolo. Pano pali Mngelo wa Mulungu ali ndi Uthenga womwewo, akuchita zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo, chirichonse chitaikidwa mu dongosolo. Branham Tabernacle, zaka twente-faifi zapitazo, pafupifupi, ine ndinayankhula pa guwa lomweli ndipo ndinakuuzani inu zinthu izi zikanati zizidzachitika, limodzi la masiku awa. Ndi izi pano! Ife tiri pa nthawi yotsiriza. Mphambano ili pano. Yayandikira nthawi yopita Kwawo ya Mpingo.

⁷⁴ Otsutsa, akupanga zotonza, akunyogodola, akuseka, monga iwo analiri ndi Mfumu Nebukadinezara ndi Belteshaza. Chomwecho iye anali mu masiku a Nowa. Chomwecho izo zinali mu masiku a Loti. Ndipo iwo akuchita chimodzimodzi lero.

“Ine sindingakhoze kuchita kanthu mpaka inu mutabwera kuno.”

⁷⁵ Ine ndikufuna kuti inu muzindikire, Loti anabwera kuchokera mu chinachake chimene chikanati chimuwononge iye, ndipo Nowa anakalowa mu chinachake chimene chikanati chimupulutse iye. Ndipo uwo ndi mtundu wa Mpingo. Ife tinabwera kuchokera mdziko, ndipo kutali ndi Elvis Presley uyu ndi m’badwo wa Arthur Godfrey umene ife tiri kukhalamowu. Tinabwera kuchokera mdziko ndipo tinapita mwa Khristu! Tinabwera kuchokera mdziko. “Iwo ndi a mdziko, adzawonongedwa limodzi ndi dziko.” Iwo omwe ali mwa Khristu adzapita Kwawo ndi Khristu. “Pakuti iwo amene agona mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa limodzi Naye pamene Iye azidzabwera.” Ife tinabwera kuchokera mdziko, kuti tipite mwa Khristu pofuna chitetezo. O!

⁷⁶ “Koma ine sindingakhoze kuchita kanthu mpaka inu mutabwera kuno.” Ine ndikuzikonda izo. “Fulumirani! Thawani!” Uthengawo unali wofulumira. “Fulumirani! Fulumirani! Thawani!”

⁷⁷ Lidalitsike Dzina la Ambuye! Yesu analonjeza kuti Uthenga uwu ukanati udzalalikidwe. Iwo wakhala ukupitirira tsopano kwa zaka ndi zaka. Ndipo pano iwo uli pa nthawi yotsiriza, chizindikiro chachikulu chotsiriza. Basi Angelo asanafuule, “Fulumirani,” Iye anatembenuka ndipo anati, “Nchifukwa chiani Sarah akuseka?” Mngelo wa chiwonongeko, Iye anati, “Ine ndamva za machimo awo, ndipo Ine ndabwera pansi kuti ndidzawone ngati icho chinali choonadi kapena ayi.” Ndipo iye anapeza kuti izo zinali zoonadi. Ndipo uthenga unali chisomo, ndi chifundo, ndi chiwombolo. Koma, “Fulumirani! Fulumirani!”

⁷⁸ O, ananu, musati mukhale chowerama ndi kumadabwa. Fulumirani! Fulumirani! Mwamsanga! Nthawi ili pafupi. Thamangirani (kuti?) kunja monga mbalame zazing’ono zinachitira, chokani ku makoma aakulu amakono awa a Babeloni, zipembedzo zazikulu zakale izi zomwe zimati, “Palibe kusiyana mu nthawi.” Mipingo yaikulu yokalamba iyi yosakhulupirira yomwe imati, “Palibe chinthu chotero chonga machiritso Auzimu. Palibe zozizwitsa.” Chokaniko ku makoma amenewo, pakuti iwo akuti aphwasuke. Iwo akupita pansi mu chiwonongeko ndi kugonja, chifukwa Mulungu wanga ananena chomwecho.

⁷⁹ Thawirani pakati pa Gologota kutaliko! Ngati mbalame zinapita ku mitengo, inu mupite ku mtengo, nanunso, mtengo uja pamene Khristu anapachikidwapo. Apo anapachikidwa pakati pa chifundo Chake, ndi kumalirira kwa Mulungu mpaka mkuntho utadutsa.

80 Fulumirani! Thawani! “Bwerani kuno, pakuti ine sindingakhoze kuchita kanthu mpaka inu mutachokako.” Iye akuyembekezera pa inu. Chokani ku tizinthu tamakono iti. Muzichoka pa televizioni iyo pamene mtundu wa masewero awo abwerapo. Tengani... Muziizimitsa wailesi iyo pamene gwedemula uyo ayamba. Muzichita monga dona. Muzivala monga dona. Muzichita monga mwamuna. Muzivala monga mwamuna. Muziyankhula monga Mkhristu. Muzikhala moyo monga Mkhristu. Mufike poyatsa milatho yonse. Fulumirani! Tulukani! Chiwonongeko chiru pafupi. Mulungu zikumdwalitsa ndi kumtopetsa.

81 O, ndi mochedwa kuposa momwe inu mukuganizira. Ora liri pafupi. Chifundo cha Mngelo, Mngelo wa chifundo Yemwe anatumiza Uthenga Wake, ali pomwe pano usikuuno. Kodi inu mukuzikhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi Mpingo udzasowa kuti upite isanafike nthawi ya Chisautso? [“Ameni.”]

82 Penyani. Israeli anapita mu Gosheni; ndipo Igupto anapita mu mdima. Igupto anakafika mu Gosheni, anatengedwera ku dziko lolonjezedwa. Igupto anapita mu mdima, ndipo anakakwiriridwa mu Nyanja Yakufa.

83 Fulumirani! Fulumirani! Thawani! Uwo ukhoza kukhala uli mwayi wanu wotsiriza. Ndipo kumbukirani, ife tikuwona mizinga itaikidwa. Ife tikuzimva izo, ife timayang’ana pa izo mu pepala. Dziko lonse likunjenjemera. Chirichonse chimene Mulungu ananena chikufika pochitika.

84 Ndiye nanga bwanji nazo? “Mu tsiku lomwe Mwana wa munthu ati adzadzulule Iyeyekha kuchokera Kumwamba.” Mwana wa munthu ndi ndani, wakhala akuululidwayo? Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Tayang’anani pa ndime ya 21, kapena ndime ya 30, ndiyo ili.

*Ngakhale izo zidzakhala ziri mu masiku pamene
Mwana wa munthu ali kuululidwa kuchokera
kumwamba.*

85 Nchiani icho? Uthenga uwu womwe... Chinthu ichi sichinayambe chachitikapo chiyambireni pamene Yesu anali pa dziko lapansi. Ndipo pano izo ziri, pamapeto a m’badwo wa Amitundu. Tiyeni tiyang’ane pa izo mphindi yokha, ndipo ganizani zolimba.

86 Pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, Iye sankadzinenera kuti anali mchiritsi. Iye anati, “Si Ine yemwe ndikuchita ntchitoyi; ndi Atate Anga. Koma ine ndimangochita chomwe Atate amandisonyeza Ine kuti ndizichita.” Yohane Woyera 5:19, Iye anati, “Indetu, indetu, ine ndikuti kwa inu, Mwana sangakhoze kuchita kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awawona Atate akuchita.”

87 Ngati inu mutazindikira Filipino, pamene iye anatembenuzidwa poyamba. Ayi...Iye poyamba atauyamba utumiki Wake, Ambuye Yesu, chinachitika nchiani?

88 Tiyeni tiwone momwe Mwana wa munthu ati adziwululire Yekha. Ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Iye ayenera kuti adziulule Yekha monga Iye anachitira dzulo. Ngati Iye ati adziulule mofanana, Iye ayenera kuti adzawulule Uthenga wofanana. Mwakachetechete, ndipo penyani.

89 Pamene Petro anabwera kwa Iye kusatira utumiki Wake, Yohane Woyera 1. Petro anayenda napita kwa Iye. Iye sanali kutchedwa Petro apo; iye ankatchedwa dzina lina. Ndipo pamene iye anayenda napita kwa Iye, Iye anati, “Iwe ndiwe Simoni, ndipo abambo ako ndi a Yonasi.

Nsodzi wachikulire uja anaganiza, “Iye wandidziwa motani ine?”

90 Ndiyeno Filipino, wochokera ku Betsaida, nayenso, iye anapita kuzungulira phiri, ndipo iye anakampeza mzake, Natanieli, pansi pa mtengo, akupemphera. Iye anati, “Tiye, ukamuwone yemwe ife tamupeza: Yesu waku Nazareti, mwana wa Yosefe.”

Penyani tsopano momwe Iye anadziululira Yekha.

91 Ndipo iye anati, “Tsopano kodi chingakhoze chabwino chirichonse kubwera kuchokera ku Nazareti?”

92 Iye anati, “Tiye ukawone.” Ndilo yankho labwino lomwe munthu aliyense angakhoze kumupatsa wina. Usati uzingotsutsa izo. Bwera, udzadzipezere wekha. O, ngati ife tingakhoze kukhala odzipereka kokha chotero, lero.

93 Ndipo ali pa ulendo wake akuzungulira, iye anayamba kumulangiza iye. Bwanji, iye anati, “Petro, dzulo, munthu... Kefa, iwe ukumudziwa nsodzi wachikulire uja?”

“Inde.”

94 “Iye anayenda mpaka pamaso pa Munthu uyu, ndipo Iye anamuza Iye yemwe iye anali ndi yemwe bambo ake anali.”

“Ha,” anati, “Natanieli, ine sindikudziwa za izo.”

95 Ndipo pamene iye anayenda mpaka kumene Yesu anali, mu mzere kumene Iye anali kupempherera odwala, Yesu anapozetsa maso awo pa iye, ndipo Iye anati, “Taonani, M’israeli mwa yemwe mulibe chinyengo.”

96 Iye anadziwa motani kuti iye anali M’israeli? Agriki ndi onse, amavala mofanana ndipo amawoneka mofanana. Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anali M’israeli? Iye anali Mulungu atawonetseredwa mu thupi. Kodi Iye anachita chiani? Iye anayang’ana ndipo Iye anamuwona iye.

Iye anati, “Ndi liti pamene Inu munandidziwa ine, Rabbi?”

97 Iye anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo, ine ndinakuwona iwe.”

98 Iye anati, “Izo zikukhazikitsa icho. Inu ndinu Mwana wa Mulungu. Inu ndinu Mfumu ya Israeli.”

99 Yesu anati, “Chifukwa ine ndakuuza iwe izi, kodi iwe ukukulupirira?” Anati, “Ndiye iwe ukhoza kuwona zinthu zazikulupo kuposa izi.”

100 Koma membala wa mpingo wosakhulupirira anaima cha pamenepo. O, molemekeza basi ndi molimba monga iwo akanakhoza kukhalira. Ndithudi. Iwo anali ataima pamenepo ali ndi maphunziro aakulu, zowachitikira zamulungu zazikulu zaku seminare. Iwo anati, “Munthu uyu ndi wambwebwe. Iye ndi Bezebule.”

101 Yesu anati, “Inu mukanena izo kwa Ine, Ine ndikukhululukirani inu. Koma pamene Mzimu Woyera ubwera ndipo ukachita chinthu chomwecho, mawu amodzi owutsutsa Iwo simudzakhoza kukhululukidwa konse, mu dziko lino kapena ngakhale mu dziko likudzalo.”

102 Kunali mkazi wamng’ono yemwe anali ndi kuwukha kwa magari. Ndipo iye anabwera kudutsa mu unyinjini ndipo iye anagwira chovala Chake, pakuti iye ananena mkati mwa yekha, “Ngati ine ndingakhoze kukamukhudza Mwamunayo, ine ndichiritsidwa.” Iye anamukhudza Iye. Iye anathamanga kuchoka mu unyinjino, ndipo anakakhala pansu, kapena chirichonse chomwe iye anachichita.

Ndipo Yesu anatembenuka, nati, “Ndani wandikhudza Ine?”

103 Petro anamudzudzula Iye. Iye anati, “Taonani, unyinjini wonsewu ukukukhudzani Inu. Chifukwa chiani Inu mukuti ‘Ndani wandikhudza Ine?’”

104 Iye anati, “Koma ine ndafooka. Ukoma, kapena mphamvu, zachoka mwa Ine.” Ndipo Iye anayang’ana pozungulira, ndi maso amenewo, mpaka Iye anamupeza iye. Kodi Iye anazichita chotani izo? Izo ife sitikuzidziwa. Koma Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo Iye anadziululira Yekha kwa fuko la Chiyuda mu chikhalidwe chimenecho.

105 Pamene Iye anabwera kwa Achisamaria, mkazi anali pa chitsime, mkazi wokondeka Wachisamaria.

106 Kumbukirani, alipo mafuko atatu okha a anthu. Ndiwo, Myuda, Wamitundu, ndi Msamaria; anthu a Hamu, Shemu, ndi a Yafeti. Ndipo Asamaria anali theka Myuda ndi theka Wamitundu. Ndipo inu mukukumbukira pamene izo zinkayamba, pamene iwo ankakwatira akazi awo, ndi zina zotero.

107 Ndipo mkazi wamng’ono uyu anabwera uko, chimene ife timakhulupirira mu dziko lathu kuti anali mkazi wambiri yoipa, koma iye sanali. Mnyamata uyu wochokera ku India akhoza kukuuzani inu izo. Ili ndi Bukhu lakummawa, ndipo

inu mukuyesera kuti muziliwerenga ilo ndi maphunziro akumadzulo.

¹⁰⁸ Pamene ine ndinapita ku India, ndipo nditatsika mu—mu ndege, ku Bombay, uko kunali abishopu a mpingo wa Methodist, ndi onse a iwo, ataima apo. Anati, “Musati mutiuze ife ndinu amishonare, Bambo Branham. Ife tikudziwa zochuluka za Baibulo kuposa inu Mayankee mungati mulidziwe konse.” Ndipo izo ndi zoonza. Iye anati, “Ife tinali ndi Baibulo zaka zikwi ziwiri inu musanakhale fuko.” Ndiko kulondola. Mpingo wa Tomasi Woyera ukadali kumeneko, kumene Tomasi Woyera anapita ndi kukalalikira. “Koma,” iye anati, “ife tikumva kuti Mulungu wakuchezzerani inu, kuti mulipange Baibulo ili kukhala lamoyo kachiwiri.” Anati, “Ndicho chimene ife tikufuna kuti tichidziwe.” Ndi zimenezo. Dziko liri ndi njala yofuna mkate wamoyo.

¹⁰⁹ Mkazi wachi Samaria uyu, pamene iye anaima pa chitsime, Yesu ananena kwa iye, “Mkazi, ndibweretsere Ine akumwa.”

¹¹⁰ Chabwino, iye anati iwo anali ndi zatsankho. Koma Iye anamulola iye adziwe kuti panalibe kusiyana. Mulungu anapanga, mwa magazi amodzi, anthu onse.

¹¹¹ Ndipo Iye anati, “Ngati inu mukanadziwa Yemwe inu munali kuyankhula naye, inu mukanandipempha Ine akumwa.”

¹¹² Ndipo kuyankhulanako kunapitirira mpaka Iye anaugwira mzimu wake. Ndiye Iye analipeza lomwe linali vuto lake. Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno.”

¹¹³ Nchiani chinachitika pamene Myuda anauzidwa izo? Myuda anati, “Inu ndinu Mwana wa Mulungu.” Ndiko kulondola.

¹¹⁴ Nchiani chinachitika kwa Msamaria pamene iye anauzidwa izo, atati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno?”

¹¹⁵ Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri. Tsopano, ife tikudziwa kuti pamene Mesiya, yemwe akutchedwa Khristu, pamene Iye abwera, Iye adzatiuza ife zinthu izi. Koma Inu ndinu yani?”

Iye anati, “Ine ndine Iye yemwe akuyankhula ndi iwe.”

¹¹⁶ Iye anathamangira mu mzinda, ndipo iye anati, “Bwerani, mudzamuwone Munthu yemwe wandiuza ine zinthu zomwe ine ndazichita. Kodi uyu si Mesiya?”

¹¹⁷ Ndipo Iye sanachite konse izo, nthawi imodzi, kwa Wamitundu. Chifukwa? Iye anazisiira izo mpaka tsiku lino. Ndi zomwe Iye ananena apa, “Mu masiku pamene Mwana wa munthu azidzadzziulula Yekha kuchokera Kumwamba.” Iye akudziulula Yekha tsopano, kwa Mpingo, mwa chifundo. Nthawi yotsatira Iye ati azidziulula Yekha, ndi mu chiwonongeko, kwa iwo omwe awukana Uthenga.

118 Mulungu akhale wachifundo kwa...kwa ife, pamene ife tikupemphera mphindi yokha. *Mofewa ndi Mokoma*, Mlongo Gertie, ngati inu mungathe.

119 Ine ndikungodabwa, usikuuno, ndikukumverani chisoni inu mwaima kuzungulira khoma. Ndipo ine ndikukhoza kumverera chiyembekezero chanu. Ine ndikungodabwa, o, ngati inu muti mukhale woonamtima kwa nokha ndi Mulungu, mphindi yokha.

120 Kodi inu mukufunadi kuti mufulumire ndi kuchokamo mu izi? Alipo Munthu mu kukhalapo usikuuno, wotchedwa Ambuye Yesu. Iye ali nacho chitupa cha inu, ndipo zonse zomwe inu mukuyenera kuti muchite ndi kungomupatsa Iye mtima wanu. Iye awutsuka iwo mu Magazi Ake Omwe, ndi kukuyeretsani inu ku tchimo lonse ndi kukaikira, ndipo adzakutengerani inu Kumwamba Kwake pamene Iye abwera.

121 Ndipo izo zikhoza kubwera usanafike mmawa, ma sputnik. Palibe chinthu chimodzi chomwe sayansi imanena...Inu mumazimva izo, tsiku lililonse, pa wailisi, pamene iwo akhala pa televizioni, pamene iwo amawafunsa asayansi awa. Iwo amati, "Palibe chinthu choti chilepheretse dziko ili kuti liphulitsidwe mu miniti iliyonse." Izo zingotengera kumwa bwino kwa Vodka, ndipo iwo adzakoka chokhethemulira, ndipo ndi zimenezo.

122 Fulumirani! Uthengawu ndi wamsanga. Fulumirani! Thawani! Thawitsani moyo wanu! Chokani kwa izo. Tulukani ku Babeloni wamakono uyu. Chokaniko ku makomawo. Kodi inu simukukhoza kumverera chinachake chikukoka pa mtima wanu? Ngati ndinu auzimu kwenikweni, ndipo Mulungu akuyankhula kwa inu! Ndithudi, ngati Iye anayankhula kwa mbalame zazing'ono zija, Iye akhoza kuyankhula kwa inu.

123 Kodi inu mungakweze dzanja lanu kwa Iye? Ife tiribe malo oti tiwayikepo anthu kuzungulira guwa. Koma ngati inu mungati mungokweza dzanja lanu, ndi kuti, "Mulungu, khalani achifundo kwa ine." Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu. O, mai! Ponseponse mu nyumbayi. Ine sindikudziwa ndi manja angati omwe alipo. "Khalani achifundo kwa ine, O Mulungu. Ili ndi dzanja langa. Ine ndikufuna kuti ndithawe, Ambuye. Mmawa usanafike, ine ndikhoza kumwa kufuulako, ine nditayang'ana panja ndipo mautaaaleza akhoza kukhala akuyandama kudutsa mmilengalenga, Mwana wa munthu angadzakhale akubwera."

124 Ndi tsiku lowopsya bwanji, kuti inu munaphonya mwayi wanu. Inu munaima kumene mozungulira mpingo wanu, sichoncho inu? "O," inu mukuti, "amayi anali a mu uwu." Ndiko konse kulondola, m'bale. Ndiko konse kulondola, mlongo. Koma chipulumutso cha amayi sichidzakutengerani inu umo konse. Amayi ankakhala moyo mu tsiku lina, ndipo inu mukukhala moyo mu lina.

125 Mvetserani Uthenga wa Ambuye, ndipo mvetserani chenjezo la Mzimu. Unali Mzimu wa mtundu wanji Umenewo, Yemwe uja amene anazindikira momwe Sarah anali kusekera mkati mwa hema? Mngelo wa Ambuye.

126 Tsopano ndi mitu yanu itaweramitsidwa, ine ndikufuna ndimupempherere aliyense wa inu.

127 Munachita chiani pamene inu munakwezera mmwamba manja anu? Inu mukuti, “Kodi izo zinatanthauza chirichonse, M’bale Branham?” Zedi chinachita. Ngati inu mumatanthauza kwenikweni izo, izo zimatanthauza kusiyana pakati pa imfa ndi Moyo. Uthenga ndi wamsanga. Kodi inu simukweza mmwamba dzanja lanu pakali pano? “Khalani wachifundo, Mulungu, kwa ine.”

128 Mulungu amdalitse msungwana wamng’ono. Mulungu amdalitse dona. Mulungu akudalitseni inu; inu, mwananga; inu, inu, mnyamata. Ana aang’onoponse kuzungulira maguwa awa akwezera mmwamba manja awo aang’ono. Chabwino, mudalitse mitima yawo yang’ono!

Inu mukuti, “Iwo sakutanthauza izo.” O, inde, iwo akutero.

129 Yesu anati, “Lolani ana aang’ono kuti adze kwa Ine, musawaletse iwo ayi, pakuti ufumu wa Mulungu ndi wa oterowo.” Iwo mwina sangakhoze kukhala moyo kuti akhale mu kukhwima. Koma, iwo adzakhala ali. Iwo sadzakhala konse. . . Iwo adzathawa, mwina, zinthu zonse zazikulu zomwe ife tiyenera kumadutsamo nazo.

130 “Mulungu, tichitireni chifundo!” Pamene inu mukukweza manja anu, izo zikusonyeza kuti pali chinachake mwa inu chimene chapanga lingaliro. Thupi lanu likanakhoza kukhala lakufa ngati pakanati pasakhale chinachake mkati mwanu, chimene chati, “Kweza manja ako.” Umenewo unali Mzimu. Ndiye inu mukukweza dzanja lanu. Mulungu wachitira umboni izo. Mzimu unakupangitsani inu kukweza manja anu.

131 Mulungu akudalitseni inu, ndi ana onse aang’ono kumbuyo uko. Ana aang’ono, achikuda awo, nawonso, cha apo, Mulungu adalitse mitima yanu yaying’ono, okonedwa. Mulungu amakukondani inu. Zedi.

132 Ife tichokako kuno, limodzi la masiku awa. Ine sindikudziwa ndi liti lomwe ziti zidzakhale ziri, koma izo—izo zikubwera. Fulumirani, mwamsanga ndithu, lowani mu ufumu! Inu mukuti, “Chabwino, ine ndinamvapo izo kale.” Inu mukhoza kuzimva izo kwa nthawi yanu yotsiriza, naponso. Lolani iyi ikhale nthawiyo.

Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, dona wamng’ono.

133 Chokani ku tizinthu tonse iti tamakono, makoma akale awa. Iwo onse agwera pansi. Gwedemula yense uyu ndi zinthu zonse izi zidzaonongeka ndi dziko. Musati muphatikizidwe mu dziko. Inu muchokemo mmenemo. Mulungu akudzera Mpingo Wake.

Iye anakusankhani inu, ndicho chifukwa Iye akuyankhula kwa inu. Uthengawu ndi wofulumira. Bwerani mwamsanga!

¹³⁴ Tsopano, pamene ife tikupemphera, khalani odzipereka tsopano ndipo mumupemphe Mulungu kuti akuchitireni inu chifundo.

¹³⁵ Ambuye Wodala, pakhoza kukhala anthu pano omwe sanayambe awonapo kugwira ntchito kwa mphamvu za Mulungu nkale, koma chinachake pansu mu mtima mwawo chati, “Kweza dzanja lako. Ndi Ine.” Ndipo iwo akuwona kuti pali kuitana kwamsanga. Iwo, iwo ndi aluntha mokwanira kuti ayang’ana pozungulira ndi kuwona kuti pali chinachake chomwe chikukonzekera kuti chichitike.

¹³⁶ Ana aang’ono, ambiri a iwo anakweza manja awo mmwamba. Mulungu, achitireni chifundo iwo. Ambiri a okalamba ndi ausinkhu wapakati, iwo anakweza manja awo mmwamba. Azaka zapakati anaika manja awo mmwamba. Iwo akufuna chifundo, Mulungu. Ndipo ndine wokondwa kwambiri podziwa kuti vumbulutso loyamba la Khristu ndi chifundo; vumbulutso lachiwiri ndi chiweruzo. O Mulungu, tikukuthokozani Inu chifukwa cha awa omwe atenga chifundo usikuuno, msewu wachifundo. “Odala ali achifundo kwambiri, pakuti iwo adzalandira chifundo. Odala ali iwo omwe amva njala ndi ludzu la chirungamo; iwo adzadzazidwa.”

¹³⁷ Muyatse nyali zawo, usikuuno, Ambuye. Mulole iwo akhale miuni yomwe yayikidwa pa phiri, yomwe singakhoze kubisidwa, koma kumapereka kuwala ku masukulu ndi malo komwe iwo ati akalumikizidwe, kuchokera kuno mpakana. Perekani izi, Ambuye. Mulole iwo akhale kuwala komwe kuti kuziwalira kwa ulemerero wa Mulungu. Adalitseni iwo.

¹³⁸ Ndipo tsiku lina, mu dziko labwinoko, Ambuye, mulole ife tonse tidzakakomane mozungulira gome lalikulu ilo la Mulungu, pa Mgonero wa Chikwati uwo. Siyani Mzimu Wanu pa ife, Ambuye. Muwadalitse iwo omwe aimirira kuzungulira makoma, ndi kunjira mu khonde ndi kozungulira, omwe akweza manja awo, ndi zina zotero. Mukhale ndi iwo, Ambuye. Iwo aima, ndi miyendo yazanzi, usikuuno. Koma, khalani wachifundo. Perekani zinthu izi.

¹³⁹ Iwo ali zipatso za Uthenga waung’ono wamsanga uwo usikuuno. Ine ndikupemphera kuti angelo a Mulungu azipange izo kukhala zenizeni kwambiri kwa mitima yawo, kuti iwo asatero—iwo asaphonye chirichonse cha Izo. Ndipo iwo ali zipatso, ndipo ine ndikuwapereka iwo kwa Inu. Ndipo Inu muwapereke iwo kwa Yesu, chifukwa iwo ali mphatso Zanu za chikondi kwa Iye. “Palibe munthu angakhoze kuwachotsa iwo mu dzanja, chifukwa palibe wina yemwe ali wamkulu kuposa Mulungu.” Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwasunge iwo motetezeka mpaka Yesu atabwera kwa iwo.

¹⁴⁰ Mulole ena onsewo afulumire, Ambuye, ndi kufulumira, pakuti Uthengawu ndi wamsanga. Ife tiyenera kuti tituluke mofulumira chiwonongeko chisanadze. Ndipo tsopano, Ambuye Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mutumize Mngelo Wanu, Yemwe uja yemwe anakhala ndi Abrahamu. Perekani izi, Ambuye. Ndipo ankakhoza kudziwa zomwe Sarah anali kuchita, mmbuyo mu hema. Ndipo uja anali Mngelo wa Pangano. Uja anali Mngelo yemwe anabweretsa chifundo moto usanagwe. Pafupi nthawi iliyonse, moto ukhoza kugwa tsopano, maatomu omwe angakhoze kuliswa dziko lonse pawiri. Mulole Iye abwere usikuuno ndi kudzapereka chifundo kwa ife, Ambuye, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁴¹ O, pali chinachake chokhudza Uthenga wodala wakale, Iwo umawoneka kuti umakutsulukuta iwe. Ine ndimaukonda Iwo.

¹⁴² Tiyeni tizingoyimba ijayi nthawi imodzi, “Mofewa ndi mokoma Yesu akuitana.” Aliyense, tiyeni tingokweza manja athu kwa Iye. Kodi inu mungachite izo?

Mofewa ndi mokoma Yesu akuitana,
Kuitana inu ndi ine,
Titachimwa, mwachifundo akhululukira,
Kukhulukira inu ndi ine.

Bwera, bwera kwanu, (Mungodzitsekera mkati
ndi Khristu tsopano.)

Otopa, bwera kwanu;
Mwabwino, mokoma, Yesu akuitana,
Kuitanira, wochimwa, kwanu!

¹⁴³ [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]... musanayambe mwakhalapo mu umodzi wa misonkhano yathu yamachiritso, tiyeni tiwone manja anu. Simunayambe mwakhalapo mu misonkhano? Izo nzabwino. Ndine wokondwa kukhala nanu pano.

¹⁴⁴ Tsopano, ine sindikudzinenera kuti ndine mchiritsi. Ine ndikudzinenera kuti Yesu si wakufa, koma Iye ali wamoyo. Sindine mchiritsi. Palibe achiritsi ayi. Khristu anakuchiritsani kale inu. “Ndi mikwingwirima Yake inu munachiritsidwa.”

¹⁴⁵ Koma ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu obwera mwatsopanonu chinachake. Tsopano, inu mwina mumapita ku mpingo. Ambiri a inu munakweza dzanja lanu nthawi ija, munakweza dzanja lanu pofuna pemphero, kanthawi kapitako. Ngati inu mulibe mpingo wousankha, ife tikukulandirani inu ku Branham Tabernacle pano, komwe M’bale wathu wokondedwa Orman Neville, munthu waumulungu yemwe saphunzitsa china koma choonadi, kuchokera mu Baibulo. Ndinu olandiridwa ku chiyanjano chathu. Ndife basi... Osati chipembedzo. Ndife mpingo basi kuno, chiyanjano. Ndife Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Apentekoste, Achilutera, ndife zonse. Ndife Akhristu omwe amakukondani inu. Ndipo ife tikupemphera kuti

tikupezeni inu... Ngati inu simungakhoze kumabwera kuno, kadzipezereni inu mpingo wabwino kwanuko, kwinkwake, kumene amalalikira kwenikweni Uthenga, ndi chotero kuti inu mukhoze kumadyetsedwa ndi Mzimu wa Mulungu.

¹⁴⁶ Ponse pozungulira, mu chipinda chonsechi, usikuuno... Ngati Ambuye Yesu anawuka kwa akufa, ndipo ine ndakuuzani inu Choonadi, ndiye Mulungu ali wokakamizidwira ku Mawu Ake, kuti awapangitse iwo chomwecho. Mwaona?

¹⁴⁷ O, musati muziwopa kuwadalira Iwo. Ziri mwina Baibulo, Liri Choonadi, kapena Ilo si Choonadi. Ngati Iwo sali Choonadi, Iwo ndi chonyenga chachikulu kwambiri chomwe chinayamba chalembedwapo, pakuti Iwo apangitsa mamilioni kunyengedwa. Ine ndaimapo, nthawi zambiri, ndi Korani mu dzanja limodzi ndi Baibulo mu lina, pamaso pa Achimuhamadi, ndi kuti, "Limodzi ndi lolondola ndipo linalo ndi lolakwitsa. Tilore Mulungu, yemwe ali Mulungu weniweni, ayankhule." Musati muziwopa. Iye sadzakulekani konse. Iye sadzakusiyani konse.

¹⁴⁸ Tsopano, Ambuye Yesu, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, ntchito zomwe Iye ankazichita, zomwe ife tangozibwereza mowerenga, Iye analonjeza kuti Iye akanati adzabwere kachiwiri asanafike mapeto a nthawi ndipo akanati adzachite zinthu zomwezo. Iye anati Iye akanati azidzachita izo kupyolera mu Mpingo Wake. Tsopano, Iye anati, "Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi." Tsopano, Mpesa sumabala chipatso. Nthambi zimabala chipatso.

¹⁴⁹ Tsopano, ngati iwo uli mpesa wa maungu, iwo umabala maungu. Ngati iwo uli mpesa wa mavende, iwo umabala mavende. Ngati iwo uli mpesa wa kantelope, iwo udzabala kantelope. Ngati iwo uli mpesa wa manyumwa, iwo udzabala manyumwa.

¹⁵⁰ Ngati iwo uli mpesa wa Chikhristu, iwo udzabala Khristu, Moyo wa Khristu, ntchito za Khristu. Mwaona? Ndiye, mizimu yathu iyenera kuti izipatsidwa mphamvu ndi chinachake.

¹⁵¹ Ndine wokondwa kwambiri kuti ndiri mwa Iye, usikuuno. Inu simukudziwa, nkhoa zapang'ono, momwe izo zikundipangitsira ine kumverera, podziwa pano, ine ndiri usinkhu wa zaka forte-eyiti, munthu wachikulire. Ndipo ine ndalalikira tsopano kwa zaka twente-seveni. Mapewa anga akugwa. Ndipo, o, ine ndikuzindikira kuti ine sindiri mnyamata wamng'ono uja yemwe anakonda kusewera ndi nsangalabwi kunja kuno ku msewu. Koma pali chinthu chimodzi chimene ine ndikuchidziwa, ndine wantchito Wake. Ine kuli bwino ndikhale ndi izo kuposa zonse zomwe ine ndikuzidziwa. Pakuti chirichonse chingachitire ubwino wanji?

¹⁵² Ine ndayesera kuti ndikhale woonamtima kwa anthu inu. Ine ndayesera kuti ndizichita chirichonse chimene ine ndikanakhoza kuti ndikhale woonamtima ndi wolungama ndi

woona, mu kukhalapo kwanu ndi mu kukhalapo kwa Mulungu, chifukwa ine ndikudziwa Iye amatiyang'ana ife nthawi zonse. Tsopano, ngati ine ndingakhoze . . .

¹⁵³ Ine ndikuuzeni inu tsopano. Uthenga waung'ono uwu usikuuno, ine ndayesera kuchokapo mofulumira, koma ine ndikupemphera kuti Mulungu atengere zina zonse izo kwa mtima wanu. Fulumirani! Fulumirani! Fulumirani! Chokaniko mu Babeloni, mwamsanga basi monga ine mungakhoze. Musati mukhale mu dziko. Chokaniko ku zamkhutu izo. Tulukanimo! Tulukani kuno, thawani, ndi Khristu. Chokani ku zinthu izo. Chifukwa inu simukudziwa ora lomwe sikudzakhala kanthu koma phulusa lokha litatsalira pa dziko lapansi, mipweya yokha, ndipo dziko lokalambali litaphulitsidwa mzidutswa. Izo zikhoza kuchitika msonkhano uno usanatseke, ndipo izo sizingasutsane ndi Malemba konse. Izo zingangokwaniritsa Malemba. Uthenga walalikidwa kale. Pano pakubwera Uthenga wotsiriza.

¹⁵⁴ Tsopano, musati muziyang'anira zinthu zazikulu mtsogolo. Amereka wachimwira kale tsiku lake la chisomo. Ndiko kulondola ndendende. Inu mulembe izo mu Mabaibulo anu ndipo mukafufuze ngati ine ndikulondola kapena kulakwitsa. Iye wakhala ali pa malo-apansi tsopano kwa zaka ziwiri.

¹⁵⁵ Billy Graham anati, pa kadzutsa wake osati kale litali. Iye anagwirizira Baibulo mmwamba. Iye anati, “*Uwu* ndi muyezo. Paulo ankapita mu mzinda ndipo ankakhala ndi wotembenuka, ankabwerera chaka chotsatira ndipo uko kumakhala kuli sate.” Anati, “Ine ndikapita mu mzinda ndi kukakhala ndi chitsitsimutso, cha otembenuka twente sauzande, ndi kubwerera mu miyezi sikisi ndipo sindimakhoza ngakhale kuwapeza mwina twente.”

¹⁵⁶ Vuto lake nchiani? Muli nsomba zochuluka chotero basi mu dziwe. Alipo ochuluka chotero omwe Mulungu anawadziwa asanakhazikitsidwe maziko a dziko, ndipo anakonzedweratu ku Moyo Wamuyaya. Pamene wotsiriza uyo abwera umo, izo zidzakhazikitsa icho.

¹⁵⁷ Munali mbalame zochuluka chotero basi zinapita mu chombo, zinyama zosiyana zochuluka chotero basi zinapita mu chombo chija. Ndipo chitseko chinatsekedwa, ndi Mulungu, ndipo izo zinawasiya iwo onse kunjira, ngakhale iwo anayesera kuti alowemo.

¹⁵⁸ Ndipo mzanga wokonededwa, ngati iwe suli mkati, iwe ulowemo pakali pano, pamene Mulungu akuitana, chifukwa zitseko za chifundo zikhoza kutsekedwa, kwa Amitundu, pa nthawi iliyonse. Tsopano, ndipo tsopano chimene ine nditi ndichite, tsopano, chikhala nacho... Chimene ine ndikuchiyankhula tsopano . . .

¹⁵⁹ Ine ndayankhula, ndipo mawu anga, ngati ine ndikanalalikirira kwa maora, izo sizikanatanthauza theka

kuchuluka kwake monga mawu amodzi ochokera kwa Khristu wathu wokonedwa. Tsopano, koma zomwe ine ndalalikira, ine mwina ndakuuzani Choonadi kapena bodza. Ngati ine ndakuuzani bodza, Mulungu sadzakhala ndi kanthu kochita nazo. Ngati ine ndakuuzani Choonadi, Mulungu ayimira kumbuyo Mawu Ake.

Ndi angati inu mukuti? Mwapereka makadi fifite?

¹⁶⁰ Ine ndikusonyezani inu chifukwa chimene ife timayenera kumapereka makadi, pamene uli ndi msonkhano wa kuzindikira za mu mtima. Ine sindikunena kuti Iye azichita izo. Iye mwina satero. Koma ine ndikufuna inu kuti mukhale owonamtima ndi ine. Ndi angati muno akanafuna kuti abwere mu mzere tsopano? Kwezani manja anu, ponseponse mnyumbayi, paliponse pamene inu muli. Aliyense mu chipinda yemwe akanafuna kuti abwere mu mzere, kwezani manja anu. Tsopano mungachite motani . . . Ndani angati akhale woyamba? Mukuona? Inu simungakhoze kuchita izo. Ife tiyenera kuti tizipereka makadi, polinga kuti tisunge—mzere.

¹⁶¹ Tsopano, iye wapereka makadi fifite. Ndipo tiyeni tingoitana kuchokera konse kozungulira, kupyola mu mulu uwo wa makadi, ndipo izo zimupatsa aliyense mwayi kuti abwerepo.

¹⁶² Tsopano, si zomwe zimachitika *pano*. Ndi zomwe zimachitika *umu*. Mwaona? Izo si, kundikhudza ine. Ndi, kumukhudza Iye. Ndi angati akudziwa kuti Chipangano Chatsopano, Bukhu la Ahebri, limanena kuti pakali pano, kuti, “Khristu ndi Wansembe Wamkulu yemwe angakhoze kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu?” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, inu mungadziwe bwanji kuti inu mwamukhudza Iye? Mwa, Iye kuyankhula movomera aponso, basi momwe Iye ankachitira. Ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Iye ayenera kuti azidziwonetsa Iyeyekha chimodzimidzi basi monga Iye ankachitira dzulo ndi kwanthawizonse. Chotero, inu mukuona, uthenga wotsiriza kwa Ayuda ndi iwo, momwe Iye ankachitira izo? Tsopano uwu ndi u- . . .

¹⁶³ Ngati Iye akanadziwonetsa Yekha mwanjira ina iliyonse, kupyolera mu chipembedzo, Iye akanakhala wosalungama. Iye sanadziwonetsere konse Iyeyekha mu chipembedzo, chifukwa kunalibe chipembedzo mu masiku Ake. Iye anadziwonetsa Yekha kupyolera mu chazimu, monga ife tinanena mmawa uno, monga cholembedwa pa khoma, kutanthauzirako. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mulungu akhale ndi inu tsopano.

¹⁶⁴ Iye anati, “Wani mpaka fifite.” Chabwino. Ndani ali ndi khadi la pemphero nambala wani, kodi mungangokweza mmwamba dzanja lanu. Tayang’anani pa makadi anu. Winawake pa machira, kapena paliponse, ndipo sangakhoze

kuimirira, aliyense ayang'ane pa khadi la wina ndi mzake. Ka khadi kakang'ono basi. Ine sindikuganiza kuti awa ali ndi chithunzi changa pa iwo, nkomwe. Iko kangokhala ka khadi kopandapo kanthu kakang'ono. Nambala wani, paliponse pomwe inu muli. [Wina akuti, "Pomwe apa."—Mkonzi.] Chabwino. Kodi inu mungangoima pomwe inu mulipo, bwana. Nambala thuu, mungakweze dzanja lanu. Dona *apa* pomwe. Nambala firii, mungakweze dzanja lanu. [Malo osajambulidwa pa tepi.]

¹⁶⁵ Ndife alendo. Ino ndi nthawi yathu yoyamba kukomana ndiye, mu moyo, ine ndikulingalira. Ndiye, Ambuye Mulungu akutidziwa tonse ife. Iye akudziwa zonse za inu, ndipo Iye akudziwa zonse za ine. Koma ngati Iye, mwa chifundo Chake, akanati akhale wokhoza . . .

¹⁶⁶ Ngati ine ndikanati kwa inu, "O, bwana, inu mukudwala. Ndipo ndiri . . . Inu mukakhala bwino." Inu mukanakhala nawo ufulu woti muzikaikire izo. Omvetsera awo akanakhala nawo ufulu woti adodometsedwe, pa izo. Ndithudi. Inu mwangotenga mawu anga okha.

¹⁶⁷ Koma ngati Mzimu Woyera ungabwere ndi kudzamuza iye chinachake chomwe iye wachichita, chinachake chimene ine sindikudziwa kanthu za icho, chomwe chakhala chiri, iye adziwa ngati izo ziri zoonza kapena ayi.

¹⁶⁸ Ndiye ngati Iye akudziwa chimene chinali, zedi, ngati uko kuli kulondola, Iye akhoza kukuuzani inu chomwe chiti chidzakhale, ndipo izo zikhala ziri zolondola.

¹⁶⁹ Inu muyenera kuti mukukhulupirira izo, Akazi a Cox, sichoncho inu? Akazi a Cox akhala apo, ine ndinangopezeka nditawazindikira iwo, ochokera ku Kentucky, cha kuno. Ndiwo Akazi a Wood . . . penapake mu tchalitchi muno, amayi awo. Khansara inali itawadya iwo nkhope yonse, *mommuno*.

¹⁷⁰ Ine ndinali kubwera kuchokera uko ku nkhalango ya kumpoto. Akazi anga anandiyitana ine, anati, "Ine sindinayambe ndamuwona aliyense atang'ambika kwambiri mu moyo wanga, monga—monga Akazi a Woods." Ndipo Bambo ndi Akazi a Woods ndi amzanga apamtima. Ndipo ine ndinapita kwa donayo, ndinabwererako ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Khansarayo inafa.

¹⁷¹ Apo, maiyo wakhala apo, ndipo inu mungalephere kuti udiwe . . . Kodi inu mungangoimirira, Akazi a Cox, kuti anthu akhoze kuwona. Mbali yonse ya mphuno yawo ndi zonse, inadyedwa ndi khansara, mpaka kufika mmaso awo. Tembenukani kuti omvetsera akhoze kukuwonani inu kumbuyo uko. Khansara.

Iye nthawizonse ndi wolondola. Iye samakhala akulakwitsa konse.

172 Tsopano, ngati Ambuye wathu Mulungu ati awulule kwa m'bale uyu, muloleni iye akhale woweruza, ngati Ambuye Mulungu wathu ati awulule kwa iye chomwe iye wadzera pano. Kapena, chinachake monga Iye anachita mkazi pa... Kapena, monga Iye angati anene monga Iye anachitira kwa Filipino, pamene Natanieli anamupeza Iye... kapena Natan... Filipino atamupeza Natanieli. Ndipo akawulula izo, kodi inu nonse mukhulupirira, anthu inu nonse mukhulupirira? Ngati—ngati bamboyu akudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za iye; ndipo ine ndakweza manja anga mmwamba, ine sindikudziwa kanthu za iye. Iye anakweza manja ake mmwamba, kuti ine sindikumudziwa iye, kapena kuti iye sakundidziwa ine. Ndiye ngati Ambuye ati awulule izo, inu nonse muzivomereza izo, mutero inu? Ndi angati? Kwezani mmwamba manja anu, kuti ine ndikhoze kuwona. Tsopano, Ambuye akudalitseni inu.

173 Tsopano, bwana, ine ndangoima pano, kuyembekeza kuti ndiwone chomwe Iye ati andiuze ine, chotero inu mukhale woweruza. Ndipo ngati aliyense angakhoze kuyang'ana, bamboyu watseka maso ake, chotero inu mukuona iko sikungakhoze kukhala kuwerenga maganizo. Mungokhala muli ndi maso anu chitsekere. Ngati Ambuye wathu Yesu... Ngati Iye ati awulule izo, ife tikhala oyamikira kwa Iye.

174 Koma bambo yemwe waima patsogolo pa ineyu, chomwe iye wadzera pano, ndi nkhani yauzimu yomwe iye akufunira pemphero. Izo ndi zoon. [Bamboyo ati, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.] Ngati uko kuli kulondola, kwezani dzanja lanu chotero kuti anthu akhoze kuwona. Tsopano kodi inu mukhulupirira? Sindinayambe ndamuwonapo iye mu moyo wanga, koma pano izo zinali. Chinachake chikusautsa malingaliro ake. Tsopano, mochuluka momwe ine nditi ndiziyankhula ndi iye, zochuluka zikhala zikunenedwa. Tsopano khalani molemekeza.

175 Kodi Mngelo uja anachita chiani? Iye anali ndi nsana Wake atautembenuza, ndipo Iye anati, "Nchifukwa chiani Sarah anaseka?"

Iye anati, "Ine sindinaseke konse."

Anati, "O, inde, iwe unatero." Chifukwa, iye anali kuwopa.

176 Tsopano ngati omvetsera angakhozebe kumalimva liwu langa, pa zotulutsira mawu. Bamboyu akuwoneka kuti akuchoka kwa ine. Ine ndikuwona mkazi ataima. Ndicho chinthu chachikulu chomwe bamboyu wadzera pano. Ndi chifukwa cha mkazi wake, ndipo iye sali pano ndi iye. Ndipo iye ali ndi vuto lachikazi, vuto la chidona, ndipo iye ali ndi vuto ndi nsana wake. Ndicho choonadi.

177 Sindinu ochokera mu mzinda uno. [Bamboyo ati, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.] Ndinu ochokera ku mzinda wina, umene umatchedwa Marysville. ["Ndiko kulondola."] Ndiko kukhoza.

Tsopano pitani kwanu ndipo mukazipeze izo momwe inu mwazikhulupirira izo. Izo zikakhala mwanjira imeneyo, mu Dzina la Ambuye. Mulungu akudalitseni inu. Mpango uwo, inu simukausowa iwo kuti ukapite pa iye; inu munali nawo iwo mthumba mwanu wa iye, koma inu simukausowa iwo.

¹⁷⁸ Ine ndikukudziwani inu. Ine sindikulidziwa dzina lanu. Koma ndinu mkazi yemwe anaima pa khomo lakumbuyo paja, tsiku lina, pamene Mngelo wa Ambuye anadza kwa ine, pamene zinali nthawi zanu zoyamba pano pa kachisi, ndipo anaulula chinachake chomwe chinali chinsinsi mwangwirowi. Ndipo inu munachiritsidwa, kwa khansara. Ndiko kulondola. [Mkaziyo ati, “Ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Koma ine ndiribe lingaliro chomwe chiri vuto ndi inu tsopano. Ine sindikudziwa. Inu mukudziwa izo. Ine ndiribe lingaliro chomwe chiri cholakwika ndi inu. Koma, ngati Ambuye akati awulule izo, inu muvomereza izo? [“Inde.”] Ine . . .

¹⁷⁹ Inu simuli pano kwa nokha. Inu muli pano chifukwa cha mwana. Ndipo mwana ameneyo akusautsika. [Mkaziyo ati, “Inde.”—Mkonzi.] Ndipo kusautsikako kuli mu nsana. [“Inde.”] Monga, sangakhoze kuima, kapena chinachake chonga icho. Ndipo ine ndikuwona makolo a mwana ameneyo, ali ndi rozare. Iwo ndi Achikatolika. [“Inde.”] Ndi banja lachikulire, ndi, azigogo awo ndi Achikatolika, nawonso. [“Inde.”] Ndipo inu mwaima chifukwa cha mwanayo. Mutenge mpango wanu ndipo kauyikeni iwo pa iye. Musati mukaikire, inu mukhoza kukhala nazo zomwe inu mwazipempha. Tsopano khulupirirani ndi mtima wanu wonse.

Inu mukukhulupirira? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁸⁰ Ine ndikuganiza dona uyu ndi mlendo kwa ine. Ndife alendo kwa wina ndi mzake, koma Ambuye Yesu akutidziwa tonse ife. Tsopano pano pali chithunzi changwirowi. Pano pali chithunzi cha Yohane Woyera 4. Mkazi wachikuda, bambo wachizungu; mu tsiku ilo, anali Wachisamaria, ndi Myuda, mitundu iwiri ya anthu. Yesu anamulola iye kuti adziwe, mwamsanga, kuti panalibe kusiyana. Ndife tonse zolengedwa za Mulungu. Dziko lomwe ife tiri kukhalamo, kusintha mtundu wathu, ziribe kanthu kochita ndi izo. Mulungu ankawafuna anthu Ake mwanjira imeneyo. Iye anamupanga munthu woyera, wakuda, wabulauni, wachikasu, wofiira. Iye anawapanga iwo mwanjira imeneyo. Iyo ndi ntchito Yake. Ndipo Iye amatikonda ife tonse. Koma pano pali chithunzi changwirowi, anthu awiri omwe sanayambe akomanapo kale, ndi nthawi yathu yoyamba, mitundu iwiri yosiyana.

¹⁸¹ Tsopano, ine ndazindikira kuti ndinu wokhulupirira. Ndinu Mkhristu, chifukwa mzimu wanu ukulandiridwa. Ndipo Mngelo uja wa Mulungu sangati alandire kanthu kalikonse komwe kali kolakwika. Ndithudi ayi. Inu mukuona

chithunzi chija apo, Mngelo uyo pa chithunzi icho uko, Kuwala uko pamwamba pa pamene ine ndaima? Ndicho chimene chikukupangitsani inu kumverera momwe inu mukumverera tsopano. Izo zikungobwera zonse pansi pamwamba pa inu.

Mphindi yokha, Mlongo Gertie.

¹⁸² Ichi chikuwoneka kuti ndi chinachake, ine sindikukhoza kumugwira donayo molondola basi. Inde. Mkaziyu akuvutika ndi chikhalidwe cha manjenje. Iye amakhala wamanjenje. Iye amagwetsa zinthu. Ndiko kulondola. Ndiyeno inu muli ndi vuto lauzimu lomwe inu mukuyesera kuti mulikonze, chifukwa inu mwakhala mukulipempherera kwa nthawi ina. Izo nzoona. Ndipo inu muli ndi nyamakazi. Ine ndikukuonani inu mukuyesera kuwuka pa kama wanu, mwapang'ono, makamaka mmawa. Inu muli ndi chinachake chovuta mu nsana wanu, aponso, vuto la nsana. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE.

¹⁸³ Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu? Inu mukumukhulupirira Mulungu yemweyo yemwe anamudziwa Simoni angakudziweni inu? Ngati Mulungu ati awulule izo, kodi izo zikupangani inu wokhulupirira wamphamvu, kuti inu mupeze chimene inu mutapeze? Iwo amakutchani inu, “Nanny.” [Mlongo ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo dzina lanu lotsiriza ndi Johnson. [“Ameni.”] Ndipo inu mumakhala mu New Albany. Mubwerere kwanu ndipo mukakhala bwino, mu Dzina la Ambuye Yesu. Ameni.

Ingokhulupirani.

¹⁸⁴ Kodi ndife alendo kwa wina ndi mzake, dona? Ife tiri. Basi kuti—basi kuti anthu awone, kodi mungangokweza dzanja lanu, ndi kuti, “Ndife alendo. Basi. . .” Tsopano Ambuye Mulungu akutidziwa ife tonse. Ndipo ngati Iye ati apereke za pempho ili, inu mukhala okondwa chifukwa cha izo?

Tsopano ena a inu mwayamba kukhulupirira.

¹⁸⁵ Tsopano, pamakhala pali munthu wachizungu akuwonekera patsogolo pa mkazi uyu pano.

¹⁸⁶ Ndi mwamuna wakhala apo pomweyo. Inu muli. . . Ziri bwino, inu mungokhala pomwe inu mulipo. Inu muli ndi vuto la impsyo. Inu muli ndi vuto la nsana. Ndipo inu muli ndi vuto la mmimba. Ndiko kulondola. Tsopano pitani, mukukhulupirira, ndipo izo sizikakuvutani inu kenanso.

¹⁸⁷ Inu mungokhulupirira. Ine ndikutsutsa chikhulupiriro chanu kuti mukhulupirire izo. Ndi angati akukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, ndiye yang'anani ndi kukhala moyo.

¹⁸⁸ Ngati Ambuye Mulungu wathu ati awulule kwa mkazi uyu, yemwe ali mlendo kwathunthu kwa ine. Ndipo awa ndi manja athu mmwamba, kuti ife sitinayambe takomanapo kale, chachidziwikire. Ndipo ngati Ambuye Mulungu wathu

ati awulule kwa mkazi uyu, ndi kuchita chinthu chomwecho chimene Iye anachita, monga mkazi pa . . . Mkazi wachi Samaria. Kodi inu nonse mukhulupirira ndi mtima wanu wonse, ndiye? Izo zikhazikitsa icho kwanthawizonse, ndi inu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁸⁹ Mukuona, ine ndiri ndi msonkhano umene ukudza. Ine ndiyenera kuti ndichoke mawa. Ndipo ine ndiyenera kuti ndipite ku Virginia, ndipo msonkhano waukulu ukudza. Ine sindikufuna kuti ndifooke kwambiri, nditaima pano. Chabwino, ine nditenga nthawi, mphindi yokha, ndi mkaziyu. Ndipo inu khulupirirani.

¹⁹⁰ Yense yemwe mkaziyo ali, iye ali ndi mdima wowoneka-moyipa ukumutsata iye. O, ndi—ndi chisoni. Inu munali ndi vuto lina posakhalitsa. Inu munataya mwana, khanda. [Mkaziyo ati, “Inde.”—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Ndipo chinthu china, inu mukusautsika ndi vuto lachikazi, vuto lachidona, ndi vuto la nsana. Ndipo inu mulinso ndi mtundu wina wa chinachake chimene chimachitika kwa inu, monga kukomoka. O, khunyu. Ndiko kulondola. Sindinu ochokera mu mzinda uno, nkomwe. Inu munawoloka mtsinje, kuti mudzafike kuno. Ndinu ochokera ku Louisville. [“Inde.”] Inu mumakhala ku nambala, yotchedwa, 1754 West Oak Street. [Mkaziyo akulira, “Inde, ine ndimakhala.”] Dzina lanu ndi Margaret Quinn. [“Inde.”] Chabwino.

¹⁹¹ Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, perekani kwa mkazi uyu chimene iye akukhumba, chifukwa ine ndikupempha mdani uyu kuti amusiye iye, mu Dzina la Yesu. Ameni.

¹⁹² Mulungu akudalitseni inu, dona. Musati mukaikire kenanso. Pitani ndipo mukalandire tsopano chimene inu mwachipempha.

¹⁹³ Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁹⁴ Inu muli bwanji, bwana? Ino ndi nthawi yathu yoyamba kukomana, ine ndikuganiza. Kodi inu mukukhulupirira Ambuye Mulungu wathu ali pano kuti achite ndi kupereka kwa inu zinthu zomwe inu mukuzikhumba. [Bamboyo ati, “Inde, ine ndikutero. Ine ndikudziwa kuti Iye ali pano. Ine ndikukhoza kumuwona Iye.”—Mkonzi.] Ine ndikusilira kulimbika kwanu. Ndipo inu muli pano chifukwa cha chinthu choyenera. [“Ndiko kulondola. Ndiko kulondola.”] Inu mukufuna musiye kumwa ndi kusuta. [“Ndi zimenezo.”] Chabwino, izo zachoka pa inu tsopano. Pitani, ndipo mtendere wa Mulungu ukakhale ndi inu ndipo ukupangitseni inumwini kukhulupirira. Mulungu akhale ndi inu.

“Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.”

¹⁹⁵ Inu mukufuna kuti muthane nalo vuto la nsana ilo? Pitani kumusi uko, mukumutamanda Iye, ndipo inu muthana nazo izo. Ingomapitani, mukukhulupirira izo, ndi mtima wanu wonse.

196 “Ngati inu mungakhulupirire,” Baibulo linatero. Khalani molemekeza. Mukhulupirire zomwe Mulungu akuchita kuti ndi Choonadi.

197 Ine ndikukudziwani inu. Ine ndingokupemphererani inu. Ine ndikulidziwa vuto lanu.

198 Ambuye Mulungu, mukhale wachifundo kwa mkaziyu ndipo mupereke chopempha ichi, chifukwa ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni. Ine sindikukumbukira... Kodi dzina lanu ndi Baker? [Mlongo ati, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Ine—ine ndikukumbukira tsopano. Mulungu akudalitseni inu. Pitirirani nazo ndithu tsopano ndipo zimukhulupirirani Iye ndi mtima wanu wonse. Chabwino.

199 Ine sindikukudziwani inu, dona. Ndife alendo. Ndiko kulondola. Inu mukufuna mukadye chakudya chanu chamadzulo, kuthana nalo vuto la mmimba ilo, nsungu zija zomwe inu mwakhala nazo nthawi yonse iyi? Pitani, mukadye, ndiye, ndipo Yesu Khristu akukhalitseni bwino inu.

200 Ine ndikukudziwani inu. Ndipo ine ndikudziwa lomwe liri vuto lanu. Inu simukudziwa—inu simukudziwa kuti ine ndikulidziwa ilo, koma, ine—ine ndikuzidziwa izo. Chotero pokhala kuti inu mumabwera kuno ku kachisi, ine sindizinena izo. Koma nyamakazi ikusiyani inu ngati inu mungati mungokhulupirira izo. Inu zipitirirani. Mulungu akudalitseni inu.

201 Tiyeni tinene, “Zikomo kwa Mulungu.” [Osonkhana ati, “Zikomo kwa Mulungu.”—Mkonzi.]

202 Ndinu wamanjenje, nanunso. Muli ndi vuto la mmimba likukuvutitsani inu. Inu mukukhulupirira kuti Ambuye Yesu akukhalitsani bwino inu? [Mlongo ati, “Ine ndikutero.”—Mkonzi.] Ndiye zipitani, ndipo mtendere wa Mulungu ukhale pa inu. Ndikungofuna kuika manja pa inu, ndi kukhulupirira ndi mtima wathu wonse, kuti Mulungu azichita izo.

203 Ndine mlendo kwa inu, ine ndikuganiza, dona. Kodi inu mukundidziwa ine? Inu mumabwera kuno ku tchalitchi? Inu mumatero. Ine sindinayambe ndakuwonanipo inu. Ndithudi, anthu ochuluka kwambiri amabwera muno. Chabwino. Inu muzipita, mukukhulupirira, ndipo vuto lachikazi ilo likusiyani inu, vuto la udona lomwe inu munali nalo. Kodi inu mukukhulupirira? [Dona ati, “Inde.”—Mkonzi.] Chabwino, ndiye zipitani, ndipo Mulungu akhala ndi inu ndi kukuthandizani inu, ine ndikutsimikiza.

204 Kodi inu mukukhulupirira, bwana? Inu mukukhulupirira Ambuye achotsa kuuma uko kwa inu, ndi kukupangani inu kukhala bwino, nyamakazi iyo? Zipitirirani kubwerera kudutsa apo, mukuthokoza Iye ndi kumutamanda Iye chifukwa cha izo, ndiye inu mukakhala bwino bwino.

205 Inu mukuvutitsidwa ndi vuto la manjenje, sichoncho inu, dona? Ndiwo manjenje aubongo. Inu mumafooka kwenikweni, mumavutika ndi kukwiya, makamaka cha ku madzulo. Ngakhale Satana wakuuzaninso inu kuti inu musokonezeka malingaliro anu. Ndiko kulondola. Koma ilo ndi bodza. Inu mukhala bwino. Si china koma basi nthawi yamoyo umene inu mukulowamo. Ndi kusintha kwa thupi. Mkazi aliyense ayenera kufika ku izo. Koma inu mukhala bwino bwino pano. Kodi inu mukukhulupirira mawu anga? Ndiye zipitani, mukumuthokoza Mulungu, ndi kuimba nyimbo ndi kumasangalala, ndi kupangidwa kukhala bwino.

206 Chabwino, dona. Ndine mlendo kwa inu, apanso. Chinthu choseketsa, pamene ine ndinanena izo kwa uyo, icho chinakusiyani inu nthawi yomweyo, chifukwa ndilo ndendende lomwe vuto lanu linali, manjenje. Tsopano inu muzipitirira pa ulendo wanu, ndipo mukakhulupirire ndi mtima wanu wonse, ndipo inu mukakhala bwino. Ameni. Pitani ndi kumakhulupirira ndi mtima wanu wonse.

207 Ine ndikukudziwani inu, dona. Ine ndikuidziwa nkhope yanu, koma ine sindiri. . . Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani inu? Ine ndikudziwa yemwe inu muli tsopano. Ndinu dona amene amabwera kuno ku kachisi. Inu mukukhulupirira Mulungu akuchizani inu? Ndiroleni ine ndingokupemphererani inu.

208 Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, mpangeni mkaziyu kukhala bwino, ine ndikupemphera, mu Dzina la Yesu. Ameni.

209 Musati mukaikire. Ine sindingakhoze kuliganizira dzina la mkaziyu, koma ine ndikudziwa yemwe iye. . .

210 Nanga bwanji inu anthu kunja kuno mwa omvetsera? Kodi inu mukukhulupirira? Tsopano mukhale mwachete kwenikweni. Mukhale molemekeza kwenikweni. Ku mbali iyi *kuno*, winawake. Ine ndikutsutsa chikhulupiro chanu, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti mukhulupirire izi.

211 Dona wachikuda ali ndi manja ake mmwamba, apo. Kodi inu mukukhulupirira, dona, kuti ine ndi wantchito wa Mulungu? [Mkazi ati, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] Ngati Mulungu ati awululire kwa ine lomwe liri vuto lanu, kodi inu muzivomereza izo? [“Inde, bwana.”] Inu mukudzifunira nokha pemphero ndi msungwana wamng’ono uyo. Kwa maso anu, mutakhala apo. Ndiko kulondola. Ikani dzanja lanu pa mwanayo, ndi kukhulupirira ndi mtima wanu wonse.

212 Ambuye Mulungu, ine ndikupemphera kuti iwo azilandire izo, mu Dzina la Yesu. Ameni.

Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

213 Pali Mngelo wa Ambuye waima pafupi ndi munthu wa mutu wakuda uyu. Ine—ine ndikukhulupirira iye amabwera ku mpingo kuno, ngakhale. Ine sindiri wotsimikiza. Bwana, ngati ine ndikukudziwani inu, ine sindikudziwa chomwe chiri chovuta ndi inu, kupatula ngati Mulungu ataziulula izo. Koma ndi zina za chifundo Chake chomwe chaima pano. Ndipo inu muli ndi—chilonda pa phazi, phazi la kumanzere. Ndiko kulondola. Chanu—chikhulupiriro chanu chakhudza chinachake.

214 Nanga bwanji inu, ku chigawo *ichi*, kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana ati, “Inde.”—Mkonzi.] Khalani nacho chikhulupiriro, ndiye. Musati mukaikire.

215 Apa, dona yemwe wakhala apa ndi chipewa chakuda, atavala magalasi. Inu muli nalo khadi la pemphero, dona? Kumbuyo komwe kwa mnyamata wamng’ono uyo apo, pa mapeto a mzere, inu! Inu muli ndi khadi la pemphero? Inu mulibe khadi la pemphero. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu? Ngati Mulungu ati awululire kwa ine lomwe liri vuto lanu, kodi inu muvomereza izo ndiye? Inu muli ndi vuto la mtima. Uyo ndi mwamuna wanu wakhala pafupi ndi inuyo, ndipo iye ali ndi vuto la amwanabele. Tsopano pitani ndi kukakhulupirira.

Ndani akumukhulupirira Iye? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

216 Nanga bwanji bambo wachikuda uyu wakhala apayu? Kodi inu mukukhulupirira, bwana? [Bamboyo ati, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? [“Inde.”] Inu mukusowa pemphero, sichoncho inu? [“Inde.”] Ngati Mulungu ati awululire kwa ine, kuchokera mwa ine kwa inu, kodi inu mumukhulupirira Iye...kuti inu mukhoza kuzivomereza izo? [“Inde.”] Inu muli ndi vuto la nkusani. [“Inde, bwana.”] Ndipo inu muli ndi chotupa. [“Inde.”] Ndiko kulondola.

217 Nanga bwanji aliynse wa inu mmenemo, kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

218 Pali mkazi wina wachikuda kumbuyo komwe kwa dona uyu kumbuyo uko. Inu muli ndi dzanja mmwamba, mlongo. Inu mukufuna chinachake kuchokera kwa Ambuye? Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Ndi vuto la mawu, lomwe inu mukuvutika nalo. Ndiko kulondola. Inu mukukhulupirira kuti Iye anakuchiritsani inu?

219 Apo pomwe kuchokera pa inu apo, kuyang’ana cha mmbali, pomwe apo kuchokera kwa inu apo pa mapeto a mzere; pafupi anthu wani, thuu, firii, folo, faifi, kumbuyo uko. Inu muli ndi vuto la kholingo. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani inu kukhala bwino?

220 Nanga bwanji kumbuyo kuno? Bambo pa mapeto a mpando, kumbuyo komwe kwa mzere apa. Inu muli ndi matumbo

azilonda. Ndiko kulondola, bwana. Inu mukukhulupirira Mulungu anakuchizani inu? Ndiye imirirani ndi kuvomereza izo, mu Dzina la Ambuye Yesu.

²²¹ Mulungu akudalitseni inu. Ine sindinayambe ndakuonanipo inu. Ndinu mlendo kwa ine. Koma Mulungu akukudziwani inu.

²²² Kodi inu mukukhulupirira izo, mmodzi aliyense wa inu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira Mngelo yemweyo wa Mulungu yemwe anabwera kwa Abrahamu, mu chifundo, Yemwe ankadziwa zinsinsi za maganizo a Sarah, Mmodzi yemweyo yemwe anaima pa dziko lapansi ndi kumadziwa zinsinsi za maganizo a mmalingaliro, kodi inu simukukhulupirira kuti Iye ali pano tsopano? [“Ameni.”] Mulungu yemweyo, basi dziko lisanawotchedwe kachiwiri mu chiwonongeko, kodi inu simukukhulupirira kuti Iye ali pano? [“Ameni.”] Ndiye tiyeni timulandire Iye. Tiyeni timukhulupirire Iye. Tiyeni timutenge Iye ngati mchiritsi wathu, pakali pano. Ndi angati a inu muti mukhulupirire izo?

²²³ Ndi angati a inu mukukhulupirira kwenikweni? Ikani manja anu mmwamba. Tsopano, ikani, muike manja anu pansu.

²²⁴ Baibulo linanena izi, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

²²⁵ Ikani manja anu pa wina ndi mzake, ndiye, ngati muli okhulupirira. Inu muzimupempherera munthu wapafupi ndi inu. Ndi mmodzi wapafupi ndi inu, kukupemphererani inu omwe mukupemphereredwa. Mmodzi aliyense wa inu, pemphererani wina ndi mzake tsopano, paliponse mu chipinda. Ine ndikutsutsa chikhulupiriro ichi.

Dona apo ali ndi TB, iwalani za izo. Inu mwachiritsidwa.

²²⁶ Inu omwe muli ndi vuto la mwera, mutakhala apo, bwana, mumadzuka usiku. Iwalani izo. Inu simusowa kuti muzikachita izo kenanso. Mulungu akudalitseni inu.

²²⁷ Ine ndikukutsutsani inu kuti mupange kachitidwe kokhulupirira. Kodi inu muchita izo? Ndiye mupemphere, aliyense wa inu, mwanjira yanu yomwe. Muike manja anu pa wina ndipo muzimupempherera wina wapafupi ndi inu, pamene ine ndikukupemphererani nonse inu.

²²⁸ Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, mwini wa Moyo wosatha, wopereka mphatso yabwino iliyonse, tumizani Mzimu Wanu pakali pano pa anthu awa.

²²⁹ Ine ndikunyoza ntchito za Mdierekezi, chifukwa Mdierekezi wayalutsidwa. Satana, iwe sungakhoze kuwagwira iwo panonso. Chikhulupiriro chawo chikukwera mmwamba, ndipo iwo ali nawo manja awo pa wina ndi mzake. Ndipo ine ndikukutsutsa iwe, kuti iwe walephera nkhondo, ndipo chiweruzo chiri pafupi. Tuluka mwa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu. Pita kuchokera mwa iwo, mu Dzina la Yesu.

²³⁰ Kodi inu mukumukhulupirira Iye? Kwezani manja anu ndipo zimpatsani Iye matamando chifukwa cha machiritso anu. Ngati muli olumala, imirirani pa mapazi anu; Khristu wakupangani inu kukhala bwino. Ngati ndinu wolumala, muli ndi manja olumala, akwezeni iwo mmwamba; izo zonse zatha.

Pano pali mkazi wolumala pano, akuimirira.

²³¹ Ambuye atamandike! Tiyeni tinene, “Ambuye atamandike,” aliyense. [Osonkhana ati, “Ambuye atamandike!” M’bale Branham akuwomba mmanja mwake kasanu—Mkonzi.] Ameni.

M’bale Neville.



KODI MPINGO UDZAPITA CHISANACHITIKE CHISAUTSO? CHA58-0309E
(Will The Church Go Before The Tribulation?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu usiku, Marichi 9, 1958, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 2002 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2002 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org